

**KUCHIRITSA  
ZIRONDA  
ZAMU  
MTIMA**

**UBWENZI UMENE MULUNGU  
AFUNA NDI IFE.**

**KEES HOEK.**

# KUCHIRITSA ZIRONDA ZA MU MTIMA

**UBWENZI UMENE MULUNGU AFUNA INDI IFE**

**KEES HOEK**

**Fatherhood Prison Ministries Fellowship International.**

Kudzera m'mapempho, kulemba uku kunasindikizidwa mu Novembala caka ca 2020. Za m'mkatimu zingajambulidwenso, koma zingalembwenso mzungunswa, kapena zonse popanda kusinta tanthauzo mziganizo, kapena kusanduliza ndi kusindikiza nkhani ngati simunapempha chilolezo ca mlembi ndipo chikazikitso ca citsimikiziro kuti bukuli silizagulitsidwa mnjira yopata phindu.

Lumikizani ndi mlembi pa email [krelishouck@gmail.com](mailto:krelishouck@gmail.com)  
webusaiti [www.FPMF.org](http://www.FPMF.org), 0977761630 mu Zambia, Kwacha  
Mvula 0962037670

Website [www.FPMF.org](http://www.FPMF.org).

Whatsapp: +260(0) 977761630  
[Emailpastorkwachamvula2005@gmail.com](mailto:Emailpastorkwachamvula2005@gmail.com)

Whatsapp: +260(0) 976214907  
[Emailgeorgezulu884@gmail.com](mailto:Emailgeorgezulu884@gmail.com)

Whatsapp: +260 (0) 976434802  
[Emailalfredtembo1975@gmail.com](mailto:Emailalfredtembo1975@gmail.com)

Whatsapp: +265 (0) 881604002  
[Emailamonbanda868@gmail.com](mailto:Emailamonbanda868@gmail.com)

## ZAMKATI

1. MAU OYAMBA.....	1
2. CHIYAMBI .....	5
3. MAITANIDWE .....	13
4. CHIMENE TIRI.....	28
5. CHIKHALIDWE CHATHU CHENI-CHENI CHA UCHIMO .....	35
6. MPHUNZIRO LA UZIMU LA MIYOYO YADZIKO LAPANSI.....	44
7. MTIMA, MOYO NDI MALO ANKHONDO YA UFUMU WA MULUNGU.....	49
8. ATATE MULUNGU NDI YESU KRISTU ACHIRITSA .....	56
9. MULUNGU ACHIRITSA ZIRONDA MUMTIMA .....	61
10. CHISANU CABWINO CA PASAKA.....	70
11. PEMPHERO LOCHIZA .....	74

## 1. MAU OYAMBA

Bukuli lidalembedwa ngati cida ca autumiki wa anthu aku Sabu-Sahala Afilika. Ziphunzitso zomverazi zayetsedwa ndi kubvomelezedwa mwa ukadaulo pakati pa anthu. Limasonyeza zakuchiza mtima wobvulazidwa, kuthandizanso anthu kuzindikira kuti kuweruza ena ndi mkwiyo ndi bvuto lofalikira pakati pathu ziri ndi mabvuto ake. Bukuli ndi njira ya bwinonso yobweretsa Asilamu kumvetsa Kolani popeza siifotokoza za choonadi ca chimo, kuzanso za cikhulukiro ca Mulungu pa ife. Ngakhale nafenso kukhulukira adani anatichimwira masiku akale.

Phunziroli ndilakuya kwa ife tonse popeza lisonyeza chindunji ca momwe uchimo ulili kwa ife, ndi momwe tingagonjetsere kudzera m'mwazi wa mwana wa Nkhosa wa Mulungu pamene tifuna Atate akumwamba modzichepetsa.

Ndzindikire ndi kuthamanda Atate akumwamba, Yesu Khristu mwana modzi woperekedwa ndi Mulungu kudzera m'mzimu woyera anadzera Mariya, mai wa Yesu ngati Yesu sanadzichepese kwa Atate ake munthu wopanda chimo, wangwiro wopanda banga, kulipira mtengo modzunuzika pa mtanda, imfa ya uchigawenga anatifera, pambuyo pakukanidwa ndi anthu, ndipo Mulungu am'chokera cifukwa sanafune kuyang'ana machimo athu Yesu Khristu anawasenza pamtanda popanda bwenzi ine **KEES HOEK** ndi Mulungu sikunakatheka kulemba bukuli.

Sichiyambi kuphunzira za Mulungu mubukuli koma “**Kumdziwa**” Iye, Wamphamvu zonse, Mlengi ndi Atate pakumfuna-funa ndi mtima wathu wonse. Colinga sikutenga zofuna zathu kwa Mulungu, koma kuganizira colinga Mulungu.

Mulungu anatilengera ndi zomwe ayembekezera kulandira kuchokera kwa ife, coonadi cathu ndi chikondi chosagawidwa chimupatsa mphamvu, chisangalaro ndi ulemerero akuyenda.

Mopitilira, phunzirori litisonyeza ngati ife, ana ake achicepere, tingathandizire atate athu kukacitika chidzetsa chisangalaro ndi mphamvu kwa lye pakumpasa chikondici. Mwaici tingathe kum'dziwa bwino ukhala naye pafupi pambuyo pakukhala woyera monga lye. Paulo analemba mauwa kwa Agalatiya **“Kufikira Kristu ataumbidwa mwa Inu”**. Adamu anali muchifanizo ca Mulungu cimene cinamcokera aticita kusamvera cifanizo, tibwerere ndi kuyamba kubwerera kwa Yesu, anatsegula njira yakwa Atate athu a kumwamba pakulipira mtengo woyenera pa ife tonse pakufa pa mtanda, kumvelera chifundo ca Atate ake.

M'bukuli muli njira momwe tingabwerere kwa Mulungu pakukhulukira adani athu pazomwe anatichitira. Mchikazikitso, Mulungu safuna kuti bwerezere zilonda m'chikumbumtima, koma tamasuka kuchipsinjo cazinachitika ndi kudzetsa chilimbikitso. Zigawo za mizimu yoipa mwa ife, zidzetsa kupempha Mulungu chikhulukiro pakuweruza ena ndi mkwiyo, tikhulukire, kupempha Mulungu kuti tikonde adani athu, cifukwa nawonso azunzidwa. Kupita muchikumbumtima camazunzo tingatheke bwino ndi thandizo la kumvera kuyerekezera ndi bwenzi lofanana chibadwe, kapena m'khristu amene athandizira anthu ndi njira iyi.

M'nthawi yanga mu Afilika, ndazindikira, ciyambi kudabwa kwanga pachikhalidwe ndi moyo wauzimu momwe uli wukulira lero pakati pa anthu mu Sabu-Sahala Afilika kufanana ndi Aisrayeli m'chipangano chakale. Kulumikizana bwino ndi Afirika nathandizika kumvetsa mau a Mulungu, komanso ine kukhala monga mwana kutenga chikhulupiriro, cabwino

pamene tikhala ndi Mulungu Atate, ambiri akhristu aciyera mu Afilika abvomekeza bwino ndi bukuli.

Aisrayeli, ndi Akristu atsopano amabwera kufupi ndi Mulungu kuti amukhulupirire, amumvere ndi kuyenda naye Mulungu, awagwiritse nchito kulemba mau ake mosamala kwa ife. Akadazindikirabe, mu mtima mwao kuti ndi Iye Yemwe, ndinso **“Iye ndi Muomboli wa iwo akumufuna modzicepetsa.”** Komanso ayenera kuopedwa ndi kulambiridwa mogwetsa nkhope zathu pansi monga Mose anathero, cifukwa Mulungu wathu, **“Sazafaniza m’njira iriyonse zolakwa ndipo azalondola mphuluphulu za Atate pa ana ndi ana ao m’mbado wa citatu ndi cinai.”** Anadziwanso kuti azafunanso chitetezo ca Iye, cifukwa Iye ndi **“Ambuye Mulungu wacifundo ndi cisomo wopilira, waubwino wochuluka ndi coonadi kusunga chifundo ku miyanda miyanda, kukhululukira mphuluphulu, zolakwa ndi ucimo”** (Exodo 34:6-8). Anthu aku Sabu-Sahala Afilika ali ndi chikhulupiriro conga ana ao angathe kubwera pafupi ndi Iye ngati aphunzitsidwa za Mulungu ndi Atate. Ngakhale Asilamu mu Sabu-Sahala Afilika, ndi a umphawi wochuluka ngati masoka a muchipangano cakhale, adziwa kuti ayenera kuopa Mulungu ndi kumupembeza ndi maondo ao opinda, nkhope zao kufika pansi molemekeza kufunitsita kumdziwa bwino. Anthu wosauka afanana ndi Aisrayeli akalewo, ndimvetsetsa tsopano cifukwa ufumu wa Mulungu uyenera wopempha-pempha wosauka wa mumzimu Mateyu 5:3, momwe Yesu anaphunzitsira, ziphunzitso za Baibulo yolankhula, amayankha bwino kwa Mulungu wao ndi mitima yao yotsweka ngati tiana, kotero kuti Mulungu wao azibvumbulutsa mwapadera momwe analonjezera mu Yeremiya 29:11-13, **“Pakuti ndiziwa malingaliro amene ndilingiririra inu, ati Yehova malingaliro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi**

**ciyembekezere. Pamene mudzandiitana Ine ndipo mudzankha ndi kupemphero kwa Ine, ndipo ndizakumverani Inu. Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse.”** Mulungu ndiwakulipira onse iwo akumufuna modzicepetsa.

Pambuyo pakuyang'ana ndi aja anthu a zauzimu mwacheru, Afilika, Ine ndemwe ndinakulabe mu ubwenzi ndi Atate anga Akumwamba ndi mosangalala kugawana nanu okondedwa owerenga inu.

**Kees Hoek**

12<sup>th</sup> March, 2019

## 2. CHIYAMBI

Bambo Kees Hoek anakulira mudziko la Netherlands m'nthawi ya nkondo yacimake m'zaka zomwe Anazi analikulanda malo m'zaka za pakati pa 1940. Anali ndi zaka ziwiri zakubadwa pamene nkondo inafika ku Holande. Makolo ake anali wokhulupirira a Dutch Reformed ndi mitima yao yokhulupirira Mulungu ndi kutumikira Mulungu wao. Chinaoneka m'nthawi ya nkondo kudzipereka kwao m'nthawi ya mayendedwe ya Adachi pansi, kumenyera kusala mitundu kopitilira ukanana ndi Ayuda usogozedwa ndi ulamuliro wa Anazi. **Kees** makolo ake anacita izi :

- Anabisa anthu aciYuda
- Anabisa acimembala amene anapulumuka m'ndege zogwetsedwa za adani.
- Anawazembetsa anthuwo ku Belguim m'njira yao ya mtendere.
- Anathandizira kubisa azibambo omwe ankhawenza m'nkondo ya Geleman – mumafakitole azitsulo.
- Anapelekanso zakudya m'zinda ndi kugulira ena anabisara.
- Tsopano, makolo anga naonso anali ndi zilonda za mtima wobvulazika cifukwa ca kulimbana pakati pao, ndiye umasiya zilonda zoononga m'mtima ya ana ao.
- Caka coyamba mu umoyo, **Kees** anagona tsiku lonse mkacipinda kapamwamba kosala.
- Ana onse anali ndi mantha kupita kukagona kuyang'anira kumene kungatulukire ziwanda m'chipinda cogona.



- **Kees** akumbuka uvimba bulangete mutu wace wonse kuopa ziwanda sizizamupeza.
- Akumbukanso ubvutisidwa m'maloto usiku wonse.

Pa msinkhu wa zaka khumi, zisanu ndi ziwiri (17 years), **Kees** anabvomera Yesu Kristu Mbuye wake, kulonjeza kumvera lye nthawi zonse ndipo mtima wace unadzala ndi mtendere kwa zaka koma zosokoneza zinabwera mochulukwa. Pambuyo pa kumaliza maphunziro apamwamba za “Mechanical Engineering”, **Kees** anatumikira mu Royal Dutch Airforce kwa zaka ziwiri polofesa injiniya ndipo pa zaka zisanu ndi cimodzi anasewenza m'migodi yosogola kukonza mafiliji, kupanga ndi kupeza madanga m'kampani. M'caka ca 1969, iye ndi mkazi, pamodzi ndi ana anai anapita ku Amerika kwa zaka zamalonda mu Amerika. Koma banja lake linakhalira mu Washingtoni ndi **Kees** akulamulira kampani yake yaikulu yamafiliji ndi yolongosola mpweya (air conditioning) kwa zaka makumi atatu ndi ziwiri. Tsopano, ngakhale anakondabe Yesu Kristu, mtima wake unanyamba kuchulutsa mabvuto pamene anali kukula, ndipo anadziwika m'migodi ya nchito yake ngati, **“Uja wopenga m'dachi.”**

Wokonedwa wake atafa ndi zaka makumi asanu ndi cimodzi (60 years), kansa yabongo inawaononga. Bambo **Kees** analandira uneneri kudzera mu atumiki asanu ndi atatu omwe sanamudziwe konse. Anati kwa lye, **udzakhala tate wa acichepere amuna amene alibe atate aiwo wokha ngakhale anayenera kusintha chikhalidwe ca mtima asanayambe utumiki.**

**Kees** anapita m'zaka zamazunzo ochulukwa ozichitira amene anadzetsa ciyambi ca kuziyang'ana iye yekha ndi kufunsa Mulungu amuthandize, pomaliza Mulungu Atate wake anayamba kusintha mtima wake, Mulungu wathu

ndiwodzicepetsa, Amene sazathero kufikira titamupempha kuthero.

Tsopano, pambuyo pa zaka zambiri, mau auneneri anakwanitsika mwapadera ndi mwakuya coyamba, **Kees** analalikira masiku onse kwa zaka zitatu m'ndende mzinda wa Washingtoni ndi azibambo ena ozaza ndi uthenga, "Businessmen's Fellowship International (FGBMFI) pambuyo pake anasogozedwa kunkha kumalo achire kumene kukhala anthu osauka. Kumwera kwa Afilika mu ufumu wa Swazilande, kumene anakhala pakati pa anthu: Kulalikira, kumanga malo azipembezo, kuyendera ndende ndi kuphunzira makhaliidwe a Afilika m'mene dziko limvetsera. Pambuyo pokhazikika pakati pa anthu akuda, masomphenya ake anabwera ku utumiki wa m'ndende, koma tsopano mu Afilika, ndipo bungwe loyendera ndende linabadwa "Fatherhood Prison Ministry Fellowship" (**FPMF**), linayamba.

M'caka ca 2012, **Kees** anatulutsa ziphunzitso m'baibulo yomvelera yothandizidwa mphamvu ya dzuwa, m'ndondomeko ya kalidzidwe linacedwa Baibulo yophunzitsa pakumvetsa (**ABT**) mwacidule ndi ziphunzitso ndi mabuku m'cingerezi, ndi chilankhulo ca Siswati ku Swazilande ndi malo akulu mu South Africa. Motero andende amamvetsera mau a Mulungu m'magulu atatsekeredwa m'ndende utsiku. Kuchokera mu 2013, **Kees** wayenda ndi nchito iyi ku Malawi, Zambia, Mozambique, Swaziland, DR Congo, South Africa, Rwanda, Ethiopia, Nigeria, Burundi, Kenya ndi Tanzania, kuonjeza m'nthawi ya Chichewa, ici Bemba, Chiyao, Portuguese, Swahili ndi Amasai kugwiritsa m'badwa zolingalira utumiki kufalitsa mabukuwa ndi mabaibulo m'ndende ndi m'midzi za muchire kumene anthu sangathe kuwerenga ndi kulemba. Ndondomeko ya zilankhulo ikupangidwa pa kulemba.

Chitsitsimuso cinamasula mu Zambia “ndende ya kupha mu 2015 pakati mazana atatu ndi makumi atatu, mphambu zisanu ndi ziwiri (337) azibambo ndi azimai, amene Pulezidenti wa Zambia anachotsa cilango conyongedwa pakhosi, kukhala zaka 25, ndipo abambo 48 ndi amai anamasulidwa pamenepo. Komishonala wothandiza anati “zopezeka mchisuloci **(ABT)** zсандuliza ndende pansi kupita pamwamba. Ndicifukwa, chitsitsimusonso cotere catenga gawo lalikulu m’midzi yakutali kumene anthu sakuwerenga. Kulingalira koyenera kusonyeza kuti pakutha kwa 2018, anthu ochuluka kuthamangira **Ku theka la zikwi** mazana awiri ndi mphambu zisanu (250 000) m’chire abwera kale kwa Yesu Khristu ndi Atate wakumwamba, pomvetsera m’magulu a anthu khumi kapena makumi atatu.

Malipoti ya zotuluka zamaBaibulo aphunzitsi pakumvetsera asonyeza kuti anthu akubwerera kwa Atate wao wakumwamba cifukwa ca chiphunzitso “**Kuchiritsa mtima wobvulazika.**” Pamene anthu ayamba kuzindikira mkwiyo umene uli mkati mwa iwo kucokera zaka za umphawi, uzunzidwa ndi mitundu yonse yakukanidwa cazona kapena uganiziridwa ndipo alondola pemphero m’ndandanda wa ziphunzitso, atamamvetsera, amamvera kumasulidwa kwakukulu kwa mtendere m’mitima yao kotero kuti adziwa Yesu ali moyo ndi mphulumutsi wona ndi Mfumu.

Mabaibulowa akonedwa kwambirinso anthu Acisilamu, cinthu codabwitsa. Buku lao Kolani siliphunzitsa Asilamu za ucimo, kukhululukira kwakhala phunziro limene siisamalidwa, koma pamene tsopano anthu apemphera kwa Mulungu, kuti akululukidwe pa kulunda kwa iwo anawalakwira kale, alandira mtendere ndipo azindikira kuti phunzirori ndiya zoono ndinso kuti Mulungu alikobe. Ayamba kuyenda m’mau a Yesu: kuti

**“Pakuti gori langa liri lofewa ndi katundu wanga ali wo pepuka”** (Mateyu 11: 30). Cithengera, atsogoleri ao masabatha owerengeka kubvomereza Yesu kukhala Ambuye ndi Mphulumutsi, koma ena Asilamu amakonda kukhala mumaMosiki ngati chitetezo ndi mboni. Iwo amatumanso ana ao ochuluka kumasukulu achikristu kumene zikutheka. Kuma Mosiki ena ama **ABT** aikidwa kuzilimba kumvelera kuphunziro la Sabatha lao.

Ku Lusaka, Zambia patapita miyezi makumi awiri pomwe Baibulo imodzi inaperekedwa kwa ma Imamu awiri kuti Mulungu achulukitse magulu womvetsera, tsopano, January, 2019, anthu opitirira 17,000 anali kumvetsera.

Tinalandira kuchokera ku Lusaka lipoti pa 23 November, 2018. kuchokera ku mtumiki wathu “Iero ndalondola m’dera la Makeni sababu utumiki wa ma **ABT**, ndapeza atsogoleri omwe ndisewenza nao apanga magulu asanu ndi imodzi m’masabatha awiri ndipo ndi okonedwa pazimene Mulungu akuwacitira, anena kuti sikotheka kwa iwo utsutsika kulondola chikhristu, koma momwe ali kuthandizira ndi Mulungu cabe.

Kulondola lipoti lamu January 19, 2019 pamene **Kees** anali kulemba bukuli: “Anamva tsopano chitsimikizo cimodzi ca Msilamu wacimuna anatha kukhululikira wina amene analumbira zaka zakumbuyo kuti sadzathero koma pakumva uthenga wa mtima wobvulazika lye anayamba kufalitsa uthenga ugwiritsa, uthenga umodzi-modzi. Ndiri wokondwa kuti anthu akulandira uthenga wa machiritso wotere.”

Anthu achifilika ali ndi ubwenzi ndi anthu ena omvetsa kuti Atate Mulungu afuna ife tibwere kufupi ndi lye, ndipo ubwenzi ndi lye udzetsa zinthu zonse kutheka. Ndaona Mulungu acita milakuli m’phemphero langa kwa anthu, koma tsopano ndamvetsa kuti

chikhulupiriro canga sichipotsa milakuli izacitika; Mulungu ayenda pa chikhupiriro ndi chichetekero.

**Kees** tsopano akulitsa chikhulupiriro cake mwa Atate ake, koma zimadza kudzera m'kupweteka kwakukulu mu umoyo wake ndi machilitso a mtima wake. Ali kucita mosayesa kucoka pamaso a Ambuye ngakhale nthawi imodzi ukacita maganizo ake kapena zomwe afuna, koma kuyembekezera kufikira Atate ake Mulungu atsegule njira, **Kees** akuti: “Ngati ndizapita patsogolo ndi kucita, ndikhala opusa pakusogolera Mulungu wanga; Iye ndi Mbusa Wabwino amene adziwa bwino kopita ndi cocita, mwaici ndaphunzira kulondola Iye.”

Nthawi yatsopano, ndilemba za bukuli pa milakuli yonse inacididwa mu umoyo wanga; Ndichula ina yochepa.

- Mu 2002, Mulungu anandifulimiza kulamula andende, amalume ake kutuluka kunjira ma sabata asanu ndi awiri (7) cifukwa ca matenda abongo, usiku umenenso adotolo anadikhira kusimikizira ndi siginechala kutseka mchini wopereka moyo. Usiku umenewu anadzuka natulutsidwa ku mchini wothandizira moyo, miyezi itatu yotsatira.
- Mu 2009, Angelo a Mulungu ananyamula galimoto mtunda ma mitala atatu pa malo otsukuluka ndi madzi pamene kunali dothi youmba yopita motsemphana ndi mseu waukulu unali ukonzedwa. Galimoto inali ukhazikika mwa ubwino tsidya lina likuyenda. Ikanawapha onse, ndipo Atate utumiki wa am'ndende kudzera mwa ife ukanafika kumapeto.
- Mu 2015, anapempherera wakhungu wandende amene diso lake linali loyera ndi pakubwerera theka la chaka, anapita kwa iwo, nkumati zikomo Mulungu anali ndi masomphenya makumi awiri ndi mphambu ziwiri, chitsitsimutso cacikulu pakati pa am'ndende okaphedwa cinacitika.

- M'caka ca 2015, Ine **Kees** ndinapempherera wolumala m'ndende woyenda ndi ndodo ziwiri, zinakhala zosathandiza, tsiku lotsatira anaciritsidwa kotheratu.
- M'zaka za 2017 ndi 2018, ulendo wa galimoto, ndinapuluma misampha yazigawenga ndi akupha, zigawenga zoipa zakupha mu Mozambique ndi Malawi zothandizidwa ndi apulisa achipupu.
- Ndingaliro za Yesu Kristu sizinasinthe tsopano; zizindikiro izi zizatsatira olalikira mau kwa osowa. Milakuli siyanga ai koma kuti osowa akulupirire.

Ndalemba maumboniwa osati ndizikweze ai, koma kusonyeza ufunikira kwakulu kwa ife kuti tikafune Mulungu ndi mitima yathu yonse ndi kufuna machiritso a mitima yathu yobvulazika. Musayembekezere momwe ndinacitira kufikira umoyo wakhala wobvutisidwa ndipo Atate Mulungu anandiitana kuti ndikamutumikire.

Mapempho ochuluka kuchokera ku Afilika ndi Amerika abwenzi ofanana, phunziro iri ndi lakucita kwakukulu, **“Machiritso a mtima wobvulazika”** kwa tsopano achotsedwa polemba.

Conde musalimbitse mtima wanu pamene muwerenga bukuli pamene mufuna kudziwa zimene mlembi anena m'mbukuli. Inde mveterani ndi mtima wotsweka, monga akkululukira adani kumacimo yakale kuti tifendere kufupi ndi Mulungu. Ngati tinena tiri bwino kwa Mulungu cifukwa Yesu analipira mphoto, sityamikira cimene Yesu Kristu anacitira kotero kuti titaye chipulumutso cathu. Chipulumutso cimacitika pamene tizichepetsa ndi kubvomereza macimo athu atsopano yomwe tacita ndipo tiri ndi cifuno cokhala woyera momwe Mulungu ali Woyera. AThesalonika 2:13, anena momveka bwino, “Mulungu anakusankhani kuchokera paciyambi kuti mukapululumutsidwe

kudzera m'kuyeretsedwa" (Njira yokhala ndi mzimu ndi chikhulupiriro m'coonadi)

### 3. MAITANIDWE

#### CHIDZIWITSO CHOFUNIKIRA

Palibe ubwino mwa ine woyenera Mulungu utembenukira, chifundo ndi chisomo. Ndifanana ndi aliyense pamene ndibvomereza kuti sindinafune Mulungu Atate ndi mtima wonse. Ndinena limodzi ndi mfumu Davide; **“Munthu ndani kuti muzimuganizira ndi mwana wa munthu kuti muzimuyenda naye.”** Nciani tsopano kuti ndizilonda Atate wakumwamba ndi kuti ndiwone dzina lake, lilemekezeke m’dziko lonse lapansi? Kodi nciani tsopano, ndiri kumtumikira Iye mu utumiki mu Afilika. Sindinamufune ndi mtima wanga wonse ndipo Mulungu ananditenga kukamusewenzera, lero, ndinena mwa coonadi kuti ndakhala opusa mu umoyo wanga posayesetsa kumfunafuna paciyambi mu ulemerero wake. Ngakhale tsopano, zirimo zambiri mwa ine zimene sizimulemekeza. Monga Mfumu Davide mu Masalmo 8:51, Atate tsopano ndawona ndi mtima wanga kuti Iye “Aika ife muni Elohim (dzina la Mulungu wathu), mwatibveka ife, ulemerero ndi ulemu. Koma ndiyambe tsopano kumvetsa tsopano. Cifukwa Mulungu mau ake anena pakumuopa Iye monga mu:

“Kuopa Mulungu ndiye ciyambi ca nzeru”

“Kuopa Mulungu ndi koyera”

“M’kuopa Yahweh ndi chilimbikitso canga ndipo ana ake azakhala ndi citetezo”

Ndinamvera kuti Iye ndi Atate anga ndipo ndi mzimu wake ndifuula kuti ‘Abba, “Liu lomwe Paulo atanthauza “Daddy”, “Pappa”, “Babba”. Chisonyeza ubwezi ndi Atate, Mulungu koposa mantha. Koma tsopano, ngati mwana wachicepere, kawiri-kawiri ndinacita mantha ndi makolo anga atakuluka nandipeza kucita zolakwika. Ndife anthu ofunikira kwambiri



ndithu ngakhale ndife anthu amalingiriro awiri, inde tiri munkhondo yauzimu mkati mwa munthu mwa ife, ndipo Atate apitirizabe kulingarira kuti ife nthawi zonse ndipo m'zonse, tisankhe kumlemekeza Iye. **“Chikondi chimabvimba machimo ochuluka”**.

Mulungu adalenga ife anthu kukakwaniritsa colinga cake mwa ife, alinazo ndingaliro pa wina wa ife koma, sindikazindikira kuti ndikanasankha kufendera pafupi ndi Iye ngati simaitanidwe ya akulu ya Iye pa umoyo wanga. Analinga uthenga njira yake ndi ine, pamene sindinazindikire Iye, kotero ankhakuwa kuti ineyu ndikhale ndi chidwi kwa Iye. Mulungu amatero kwa anthu ake pamene afuna kuwasewenzetsa ndi omukonda Iye, ngakhale ndi maucimo akulu mu miyoyo yao. Panopa zitsanzo za m'baibulo.

Mose anathawa kupulumutsa moyo wake atapha m'Aigipito, amene Mulungu anaitana m'chitsamba ca moto mwa ndingaliro yaikulu mu umoyo wake kukatulutsa anthu a Mulungu a Israyeli mu ukapolo ku mtendere m'malo olonjezedwa. Koma ankanapita mum'sintho wa khalidwe coyamba kuti akazichepetse akafewe ndi mbusa wodekha kuposa ukhala mfumu yozikhuza ndi ya mkwiyo woipa emwe adalakwa mu umoyo wake. Izi zingatengera zaka makumi anai (40) za umoyo wake, koma pa nthawiyi, Mulungu adakonda kulankhula naye “Nkhope ndi nkhope,(Numeri 12:7-8)

Yosefe, uja wozithamandira, m'nyamata yemwe anaganiza kuti angaphunzitse abale ake akulu kufikira anadana naye, koma ndiye yemwe Mulungu anaitana kundingaliro yake yodabwitsa kuti akateteze mbeu YOLONGEZEDWA YA HEVA, ndikusimikizira kuti lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu akakwaniritsidwe, kotero kudzera mbeu yake anthu onse padziko akadalitsike. Yosefe nayenso anayera kusintha

khalidwe ndi kuphunzira kudalira pa Mulungu wa Atate wa Israyeli koposa iye yekha, ndipo kunayenera ukhala zaka khumi ndi zitatu (13) ngati kapolo mundende koma mofatsa ndi mwanzero iye anakhalira kukhululukira abale ake ndi mtima wonse pamene anati kwa iwo, “Musaope, cifukwa kodi ndiri m’malo ya Mulungu? Cifukwa inu, munandicitira ine coipa, koma Mulungu anachisanduliza ubwino kuti akasunge anthu ambiri ndi moyo, musakhale ndi mantha, Ine.

Davide, amene makolo ake khumi anabwerera ku Yuda sanalodedwe kubwera pamaso pa Mulungu, ndipo anakhalanso wakupha. Koma Mulungu anamuitana kuti abweretse anthu ake a Israyeli kufupi ndi mtima wake; kumukonzekera kuti akhale Mbusa wa anthu a Mulungu a Israyeli, amfumu, aneneri ndi mlembi wa nyimbo zolambira zauneneri za Israyeli mu ulemerero wa Mulungu.

Paulo, amene anazicha wocimwa kwambiri koposa onse, analinso wosankhidwa kukwaniritsa ndingaliro ya Mulungu kuti akonze gawo yaikulu ya Chipangano catsopano ndizakupatsani kuti mukhale ndi moyo ndi achicepele anu; mwaici anawathokoza nalankhula nao mwachikondi” Genesis 50:19-21. Koma cingatengera kukumana mwa, Mulungu ndi mwapadera ndi Yesu kuti iye atembenuke ndipo mazunzo ake akasinthe khalidwe lake pofuna kukhala kapolo wa Yesu.

Pali anthu ambiri amene anaoneka osayenera kwa Mulungu moitana pandingaliro zao, koma lye ndi woumba mbiya ndipo ndife ndinthu m’dzanja lake atikonza kuti akatigwiritse nchito kukamaliza colinga anatilengera mwa ife osayenera kudalirika, timamvera odalitsika pamene tizikhutura kundingaliro yake.

Chifukwa ine ndinayankha? Sindinakatero koma kumvera kuchokera posayankha komanso kuchokera mkuopa posayankha momveka bwino kwa Mulungu. Ndakhala

odankhawa ndipo ndinafunsa Mulungu kuti, “Chifukwa Munandisankhula ine, munthu wobvutisa ngati ine amene mobwereza-bwereza waphweteka anthu ochuluka, ngakhale mkazi wake ndi ana? “Tsopano ndazindikira kuti umoyo wanga wakhala chikonzekero ca utumiki wa lerori, ngakhale sindinazindikire cimenezi. Mwaici ndikusogoleredwa kupereke chiphunzitsa ca **kuchiritisa mtima wobvilazika**, ndakhala ndi kupita m’zimenezi. Kumatumikira Mulungu kumafunika coyamba uturutsa chinyengo ndi mkwiyo mu mtima. Kodi ine ndinamvetsa makhalidwe anga? Ai, nanga machiritso ankhacitika motani pokhapo Mulungu lye yekha acita mogwirizana nane, lye anadziwa zinafunika kuti zichiritsidwe.

M’zaka za 1997 ndi 1998, pamene mkazi anali kufa ndi nthenda ya kansa wa bongo, Mulungu anacita milakuli kwa ife pamene ndikanamlirira pa cifundo ndi machiritso yake cifukwa sindinaone kukhala popanda mkazi wanga paciyanbi machiritso anali ochuluka pa iye modabwitsa ine, banja langa ndi a dotolo.

Koma imfa ya mkazi wanga yosayembekezera, Atate Mulungu anandibweretsa ine kwa lye yekha kotero ine ndinamkonda koposa nthawi zonse ndipo ndinati kwa lye “Ambuye, mutenga wokonedwa ndinali naye, ndipo tsopano ndikukondani makumi awiri kochuluka, mukhale Mulungu wokwaniritsa kukacita tero. Koma simunandipatse moyo wake? Munatipatsa caka catha zonse tinakupemphani? Tinalibe chizolowezi cholandira mayanko mokuwa ndi momveka bwino kuti **“Unakonda mkazi wako koposa ine ndipo ndinafunika kukusewenzetsa nthawi zonse.”** Uyu unali uneneri woyamba wa maitanidwe anga, woperekedwa kwa ine mwacindinji, ndipo ndikumbukiranso pamene ndinali ndi zaka 18 ndinamva maitanidwe anga amene anakhala mkazi wanga kwa zaka makumi anai ndi mphambu ziwiri (42) tiri pamodzi. Tsopano ndinakhetsa misozi ndinati

“Atate ndiri cisoni kucokera tsopano ndidzakhalapo na Inu. Theka la miyoyo izabwera kwa Mulungu, izabweretsa chichetekero. Ndiciyembekezo ndinadikhira njira ya cisogozo.

Ndipeleke pakati conena canga pa zimene ambiri ainu amamverera. Mkazi wanga sanalandire chilango cake kwa ine, mkazi wanga anati masabatha anga asanapite ku ulemerero wake “**Kees, nditamvera bwino, tikapita limodzi ku nchito ya autumiki.**” Iye anakhala m’neneri mu nthawi ya masauso ake ndipo akanazionanso wamphumphu ndi mu utumiki ndi ine. Ndisimikizira kuti ziri concu, kuti anaciritsidwa ndipo ali ndi ine m’nchito ya utumiki m’maiko kukhala opembedzera wanga, anakhala Mulungu umodzi anagwiritsa nchito kuteteza ine kuti ndikagwiritsidwe nchito ndi Iye tsopano, m’zaka zotsatirapo pano padziko. Kodi kudzitamandira nkhwa zoonadi? Lero lino, ndiri cimene Atate Mulungu anandipanga kukhala kuti akandigwiritse nchito ku ulemerero wake.

Tsiku la 14 June 1998, miyezi iwiri atapita ku nyumba ya Atate wake, ndinalandira uneneri waciwiri kuchokera kwa mlaliki wolankula ku chalichi wathu. Pambuyo pa mapemphero ya madzulo anaitana anthu anali ndi mabvuto olumikizana kubwera kutsogolo kupemphereredwa. Ndinauza Atate Mulungu, nkhwabwino ndilandire uneneri weni-mweni wazoonadi kuchokera kwa Inu kuposa machiritso a nsukunya zanga; Ndinafunitsitsa chitsimikizo ca maitanidwe a Mulungu pa moyo wanga pomwe nasimikizira kupita kwa mkazi wanga ku nyumba, yakhala ndingaliro ya Mulungu. Pamene mlaliki anabwera kwa ine sindinanene cinthu pa imfa ya mkazi wanga kapena kufuna mau ochokera kwa Mulungu, Atayamba kupemphera, mwacidziwikire anandidabwitsa pamene uneneri uyu unanifika **Kees!** “Ndinaciona cophwetekeka, koposa la kumanzere ili yoipa”

**Keith:** “Inde, cabwino, Kodi Mulungu azakuchiritsa liti?”

**Kees:** Mochedwa ndipo onse anaseka.

**Keith:** Muli nako kubvutika m’bale koma ndine okonzeka kuyamba, concu, tizaona cimene Mulungu azacita, cabwino.

**Kees:** Ndidziwa azacita tero, ndinganene kuti: “Mulungu, bwerani muthandize cisakhulupiriro canga” Ici ndi cabwino ndinganene.

**Keith:** “Ndimwe olungama ndipo Mulungu adzakumana nanu pamene muli, Ameni?”

Tsopano lino halleluia!”

Motsatira codabwitsa cinatsatira: “Ai sikuti, koma Mulungu ali ndi colinga pa inu. Mulungu akuitanani kuti mukabweretse kubeleka, kuyendetsa thupi pamene muzaima mumphamvu yanga, kumene chino chaka, ngakhale iwo amene apereke kubwerera ndipo kuyenda kwa tsopano ndi ulemerero watsopano wa Mulungu wa tsopano lino, ndiyamike Yesu.”

Kumagwira m’ciuno, kumapita kumalo a kavali, kumene Yesu ananyamula matenda awa ndi mokuwa analamula nati “**Kwatha.**” Ambuye pa nchito ya mwana wanu ndi panchito yomaliza pakali, kudzera m’mikhwingwirima yake panali machiritso ndi kutulutsa matemberero onse m’dzina la Yesu, Zikomo Ambuye Yesu, cifukwa ndasankhanso Inu kuti ndikhale olimba ndi Imwe, ndipo mudzatsutsa adani anga onse amene atsutsana nanu kuno cifukwa m’mau ndi m’mau amene ndakupatsani mudzakhala chishango ca chikhulupiriro ndi mibvi yolasiidwa ndi m’dani siizakuzunzani. Musafoketsedwe popeza pali mapemphero amene saoneka kuti anayankhidwa. Koma mwapambana ndithu ndi Mulungu ndipo munamvedwa ndi

Mulungu. Ndipo cinali ndi utumiki wanga Yakobo, muzasinthidwa kukhala Israyeli (**kutanthauza mfuulu wa Mulungu**) ndipo mudzamuka kupita ku malo achigonjetso.

Zikomo Inu Yesu, zikomo Inu Mulungu. Waona ulemerero wanga ndi udzawonanso ulemerero wanga pakuti ndizatenga mbali yako. Usachite mantha. Zikomo Yesu, Zikomo Inu Ambuye. **Amen.**

Yendani muzungulira chiuno, mumvera kanthu kalikonse? Mumvera mphamvu ya Mulungu? Ndinamvaponso mphamvu ya Mulungu. **“Tsopano ndiona chifukwa chifuno chiripo”.**

**Kees:** Ndinamvera, ndinamvera chikondi ca Mulungu.

**Keith:** Inde, ici chakhala, cifukwa ndi kumbuka nchafu ya Yakobo, pamene anatuluka pamalo, panali kugwirira, koma Yakobo anapita ndipo Mulungu adzacita zotheke kuti uwone mphamvu imodzi-modzi ndi chionetsero ndi kutsintha kwa khalidwe ndikupita mtsogolo. Kuchokera nthawi yomweyi, sindinamvetsa kuphweteka m'chafu yanga yakumanzere pamene lakumanja inachiritsidwa kotheratu.

Chotsatirapo, m'madzulo pa 9 February, 1999, ma uneneri anai anaperekedwa ndi anthu sindinazindikire, ndipo m'masiku ochepa atatu. Ndinali kunyumba ya mapemphero, kumene mlendo anati kwa ine, **“Kees,** ndikumva Ambuye kundiuza kuti udzakhala **tate** wa ana achicepere anymata amene sanakhala ndi **atate** aiwo wokha, udziwa, cifukwa iye akhala utanganidwa, kumva mochuluka kuchoka pakhomo ndi madzulo otsatira, cisanafike chidzulo ca tsiku lacityatu usiku mapemphero adayambika, ndiyenda kubanja latsopano m'chalichi kukawonetsa zithunzi ndinawajambula kuchokera m'chisogozo cha chalichi yathu. Anayang'ana pa ine mopyola **nati, ndiri**

**kulandira kwa Ambuye kolona ya utate pa ine ndi kolona ya upostoli ndi utumwi**, wobyala mipingo ndipo zimenezi zizakhazikitsidwa. Analankhula mwakuya mwakanthawi koma izi ndi zomwe ndikumbuka tsopano.

Usiku uja anadza ngati chodabwitsa cacikulu pamene mneneri wacikazi wodziwika bwino m'dziko lonse analankhula, sindikumbuka ulaliki wake, analoza cala cake pa ine nati, alinane mau ochokera kwa Ambuye. Panali anthu ochuluka onga mazana atatu (300) koma anandiitana pakati pao. Uneneri wake unayang'ana pa maitanidwe anga ndi zochuluka pa kuchiritsidwa kwa mtima wovulazika wanga kukhala cinthu coyamba kucitika. Sindinamvetse gawo iyi coyamba. Zolemba zomwe Mulungu ananena nane ndi izi:

Ndikhulupirira, kuti sitsiku lake cabe ili m'kudza ai, koma tsiku iri nkudza pamene chikumbo ca mtima wako cidzakwaniritsidwa pamene panakumudwitsidwa; ngakhale kumene maganizo ako anakuuza; Ndizosatheka: kudzakhala nthawi imene udzamva Mzimu Woyera kunena kuti: **“Ine ndine zoonā Mulungu wacosatheka.”** Ndipo ndiwokonzeka kuyenda m'malo ako ndi kucita zosatheka kuti ukaike ndondomeko; nkosatheka kuti ukaziombole wekha m'nyengo zomwe upitamo; chidziwikire nkosatheka ndipo lye adzaombola comwe ciri cake mwa iwe.

Tsopano, pamene wakhala woyeretsa iwe pali zigawo sizake ndipo zakhala zophweteka, koma ndizocitika zomwe aliyense akhala wopitamo kukakwaniritsa; mwayi siusiyana ndi wina waife.

Udziwa, pali zinthu zochuluka mu mtima mwako zomwe zadzadza munsu umo kwa nthawi yaitali, ndipo zina zabwino ndipo ziyenera kubwera mtsogolo. Inde, pali zinthu zabwino zambiri, zabwino zambiri. Liu lina ndinamva monga kwa inu, linali kuti utapita m'zonse izi ndikumagiriza mtima mwako,

kotero ukhale ndi mtendere mtima mwako, mulibenso m'tsutso ndi kudankhawa, kuti uzakaphunzitsa ena, achicepere, ochuluka amuna achicepere, ochepa mwina angakhale tsopano, palibe cina moonga wukuundatira, uzadzakhala naco tsiku lina ndipo inde cidzakhala cabwino, ndipo uli nazo zimene ziyayenera osati zimene afuna, cifukwa.....”

Ndinali odabwitsika kotero ndinalephera kuziongolera ndipo ndinalankhula naye nati “Wow, iyi ndi nthawi yacitatu kuchokera usiku watha kuti sindilimbikira, kulandira uneneri kuti ndidzakhala atate kwa amuna achicepere.

Pa cisanu mu February 12, 1999, pa chakudya uthenga wa “Businessmen’s Fellowship International” m’mulankhuli wa mkulu wa tsiku lija, bambo amene sindinakomane naye kale, analankhula mau ake mofanana ndi m’neneri uja adacita pa usiku wa tsiku la citatu, kuloza cala mofulumira pa ine. Pano pali lemba la mau ake:

**“Ndiona kuti pali chizozo ca utumiki cimene ukuyendamo,** ali Kolona amene azadza pa iwe ndipo adzakazikika, sicizakhala cinthu cimene uzaika pa iwe kapena kuchotsa koma kuyenda, mu ulamuliro wa utumwi, anali mphunzitsi wako pa cilengedwe. Aphunzitsi amanena zinthu m’njira yakuti wina angathe kulandira ndi kukhulupirira ndikudyetsedwa kuchokera kuzolankhulidwa, inde ndipo cimene chikubweretsedwa kwa inu ndi nsalu ya kuphunzitsa, Mulungu akuinyamula pamene mukupita, idzanyamulidwa kwa, iwe; chidzakhala ngati uzaimba mkati uzatenga cisinsi ca mau a Mulungu, usasiye zinthu zing’ono. Iyi ndinyengo ya Mulungu ndi comwe Mulungu alankhula chalichi iyi, kugulu la anthuwa kusukulu iri. Cabwino? Ici, mwina ndikumene Mulungu afuna kukutuma ukayambe kulankhula ndi kulalikira, cabwino? **Zikomo, Ambuye.** Chidzozo ca utate ciri pa iwe ndipo ndikumbutsidwa malemba



m'mene Yesu anati: **“Yemwe ali mai ndi tate ndi mbale ndi mlongo, ndi iwo amene acita cifuniro ca Atate yemwe anandituma.”** Ndi anthu ochuluka; atate awo adziko mwina anawasiya mwina akhala otanganitsidwa, mwina anawagwiririra ndipo ubwenzi wao unaonongeka ndi Mulungu Atate wao Wakumwamba. Mulungu akupereka danga lakukonza ubwenzi ndi Atate wanu Wakumwamba, osati cabe ndi Mzimu Woyera koma ndi Yesu. **Zikomo.Ambuye.**

Ndikuona masukulu ochuluka ali kukudzidwa, monga ana achicepere. Ndikuona ngati siuzapita ndikukamanga masukulu awa eni-eni, **ciri monga uzapita kukayendera ndikuyala madziko m'mitima ya aphunzi.** Ndikuona achicepere kukhuzidwa.

**Ho!** Ndikuona nsomba ikanzingidwa mupani, ndi chakudya ca achicepere kuti akadye. **Oh!** Koma tsopano ndikuona iwe kukhala nsomba ija!

Ndikuona mayankho ya ukachenjede. Mulungu azakuyankha, udzakhala woyamba kulandira. Yali monga mayankho kumabvuto pambuyo pa zinthu kutengedwa kwa ife, zimene tsopano tizidzindikira; ingakhale monga ndondomeko ya intaneti yimene ingalamuliridwe ndi m'dani; ngakhale kulumikizana m'njira za matelefoni, setelaiti. Koma Mulungu akucita zatsopano mtima mwako ndi m'maganizo. Ndinaona maganizo ako kuoneka ngati kompyuta ndipo ndiona Mulungu mkati umo ziri kusintha akalipentala, kumphamvu zochuluka ndi kuonjeza mphamvu zako kukagwira, kumvetsa ndi kupereka chija cimene ali kupereka kwa iwe, cifukwa angakuchetekere. **Zikomo Ambuye, Halleluya.**

Chidzozo cako cikakupitirira, pali monga ciyembekezo pamene ufika paja. Zidzatengedwa ndi chikhulupiriro kuchokera kuzimene udzawapatsa. Padzakhala ulemu pa cidzozo ca

utate pa umoyo wake. **Zikomo Inu Yesu**, halleluyah, zikomo Inu Ambuye.

**Ho**, udzakhala nyali ya moto wachitsitsimutso kujako, m'bale wanga; moto wachitsitsimutso, moto wachitsitsimutso ndipo ndikuona tsopano wacisanu kwa tsopano, inde, moto wacisomo, **Zikomo Inu Yesu**.

**Uneneri** wothera ndifuna kupereka ndiwochokera kwa mlankhuli wina, ndipo pa cakudya ca FGBMFI pa May 21, 1999; kuchokeranso kwa munthu amene sindinadziwe kale lomwe ndipo sindinapempheko uneneri mwina.

Ambuye akunena kuti: **"Mwana Ndikumanga mphamvu mwa iwe zimene ukusowekera**, ndipo nthawi imodzi-modzi, Ambuye akunena nane kuti akumanga kuyang'ana zinthu mu m'zimu mwa iwe, chinthu capadera kuti udzatha kuzindikira zichitidwe zina zimene anthu abwerera ndi zolinga zao. Ambuye akunena uzalandira diso la kusala, sindiyekuti uzasala anthu ai, **koma uzasala kuwala kuposa m'dima**. Kodi umvetsa ici, kuwala kuposa m'dima? **Ndipo uzatha kuwerenga pakati pa maganizo a anthu**: zimene akunena ndi m'mene iwo aliri. Ambuye akunena uzapita kukadziwa ici, **uzatumikira mkuwawa mitu**, utaya nthawi, ndi cuma cifukwa udziwa kudzikira maganizo ya anthu ndi zomwe ukalankhula, chikhala ngati uzapenya m'mitima yao ndi maso yao yakhala openyeka ngati galasi ya madzi mwa iwe ndipo iwe uzadziwa pamene muli mdima mkati-osati siali odabwa kwa tsopano, koma pamene muli cinthu colakwika. Ndipo Ambuye akunena; **"mwana wanga, ndiye pamene ulankhula choonadi ndi chikondi nthawi zonse ndi mtima wogulidwa kwa iwo."**

Sindidziwa, sindidziwa cocita, **koma Ambuye akunena uli nawo mtima wa Mbusa**. Ndipo Ambuye akunena: **Mwaici**

**siunandilepheretsa ine, atero Ambuye, koma ndikupatsa iwe mphamvu, atero Ambuye zimene unalibe kale.**

Cimene Ambuye akunena kwa ine, wakhala uli kumvera kuti pali cinthu cikusowekera mu umoyo wako, kusowekera kwa **chikondi**. Ndipo Ambuye akuti “**Ndilore ndizadze m’kucha, opanda kanthu kuchokera kale cifukwa ndakhala osati Atate wako cabe, komanso bwenzi lako ndipo kupambana apa, ndakhalanso m’nomfu wa m’nomfu wako ndi fupa la fupa lako. Ndine wako, atero Ambuye, Amen, Amen.**

Kodi muzindikira kuti ndime ziwiri zothera za uneneri zinena pa kuchiritsidwa kwa mtima wobvulazika? Chiziwikire sindinazindikire za ndime yothera imeneyi mwina m’nthawi imene sindinadziwe za mtima wanga ndi zilonda zake.

Ndinapita ku m’khristu wolangiza kuti akandilangize pa bvuto ndinali nayo ndi bwenzi langa labwino, kucetekera kuti azabwera nane limodzi ndipo anatero. Koma m’misonkhano yochepera, Mzimu Woyera analankhula nane pa thandizo yomwe ndinafunikira, pothera Mulungu anayamba kundikonzekera, “**kusinthwa kwa khalidwe**”, imene ndinalandira mu uneneri, mobwereza-bwereza. Ici cinakacitika maka ndisanayambe kutumikira Mulungu kulingana ndi ndingaliro yake. M’nthawi ya zaka zitatu, ndinalalikira m’ndende pafupi tsiku liri lonse mu Washintoni pamene ndinali kulandira maphunziro abaibulo ndi kuchiritsidwa kwa mkati mwa m’mtima ndi kulandira maphunziro a malangizo kapena kuloweza maphunziro asaikoloje.

Ndipo m’chaka ca 2003, Mulungu anandisogolera kawiri ku ndende yaku Swazilande, kulalikira m’malo akuthengo, kuthandizira azibusa amadera awa; kuyambitsa misonkhano ya mapemphero, ndi kuyendera ndende kugona m’malo amenewa ndi anthu. Ndinayamba kuphunzira khalidwe la anthu akuda ndi

malingaliro a anthu m'dziko lapansi. Atate Mulungu, ndisonyezeni zina za anthu awa afuna kudziwa kuti asinthe chikhaliidwe coipa, maganizo oipa amene apasa satana kukhala ndi ulamuliro pa Afilika. Mwatsopano ndinayamba kuphunzitsa mtima wobvulazika.

Zaka zambiri tsopano phunzirori lakhala cimake maphunziro anga mu ulaliki, pothadiza anthu ukhala pafupi ndi Mulungu, kuti Mulungu ayambe kuwasewenzetsa mwa ndingaliro za Mulungu. Afilika ndi anthu opanda tsanko pa chikhaliidwe, pakuwafikira iwo, chaonetsa poyera kuti ndi phunziro lodalirika koposa kuwaphunzitsa nkhani za m'baibulo ndi maphunziro a ubusa wansembe, ndikuwaitana iwo kupempha Yesu kuwakhululukira macimo. Mu 2011, ndinasogozedwa kukasintha masewenzedwe anga kukhala am'ndende okha tsopano kuyambira mu Swazilande, komanso Malawi ndi Zambia. Ndiye pamene utumiki wa Fatherhood Prison Ministries Fellowship (FPMF) unayambika.

Kubweretsa seminala ya masiku atatu m'ndende m'njira yathu, tinali nako kucita kwakuti, ndinayamba kuzindikira uneneri wa zaka za khumi ndi ziwiri zinakwaniritsidwa. Mulungu, Iye Mwini anali kugwira nchito, ngakhale mwaine.

Anandipasa ine masomphenya kuti ngati ndizasiya Baibulo yolankhula m'chipinda ca ndende ciriconse momwe tinamaliza seminala, wokhuzidwa andende angathe kukhala kufikira kwa Mulungu atatuluka m'ndende.

Conco, mu 2012, ndinatenga nthawi yaikulu kulemba ndi kujambula ziphunzitsa mu Afilika ndi kuziika mukachisulo kamene tinakonzera ndondomeko ife temwe ndi ziphunzitsa ndi Baibulo yakutha, coyamba m'chingerezi ndi Siswati kapena Chizulu, kutsatira ndi zilankhulo za mu Zambia, Malawi ndi ku mphoto kwa Mozambique.

Mu 2015, chitsitsimutso cacikulu cinayambika m'mandende ochuluka mu Zambia kotero iwo anali m'ndende kukaphedwa, milandu yao inachepetsedwa zaka kucoka kuimfa kufikira zaka 25 ndipo anthu 337 andende, okwanira 48 anamasulidwa.

**Kunali kuti**, nthawi iyi Mulungu analankhula nane momveka bwino nati anthu a kumidzi yakutali omwe sankhawerenga anali ndithu mu ukapolo wa satana monga andende aja ndipo anafunika kumasulidwa nawo. Tinabweretsa mabaibulo wolankhula **(ABT)** m'malo a midzi m'Malawi mu 2015 yanaperekedwa ku magulu omvetsera anthu pakati pa 10 ndi 30 m'midzi ya akhristu ndinso Asilamu ndi tinaonanso chitsitsimutso cacikulunso, kuthandizira mipingo kukula kupititsa patsogolo ciwerengero ca anthu. Mu October 2016 tinapereka mabaibulo kudera inanso ku Mozambique. Tikupitirira lero, March 11, 2019, Asilamu 250,000 ndi Akhristu nawonso abatizidwa kuchokera paciyambi tilandiranso ma lipoti ku Lusaka, Malawi, Nyasa ndi kumwera ndi kum'mawa ku Tanzania, ma Mosiki akulumikiza mabaibulo a kuzilimba kuti cipembezo conse amvetsera pamodzi. Madera odzicha Akrisitu achitanso cimodzi-modzi.

Kuchokera nthawi tinabweretsa Baibulo iyi nthawi yoyamba Asilamu Imama mu Lusaka, likulu la Zambia zaka zapitazi, kuli Asilamu 17,000 ali kumvetsera pamodzi m'magulu mu Lusaka cabe. Mulungu wathu ndiwodabwitsa m'zinthu zambiri pakati pa ana ake muno mu Afilika. Azabweretsa kukolola, ngati sikutero.

Zotulukira zadziko zatha kulambira lye, azawabweretsa mkati kuchokera kumiseu ikulu ndi njira zina. lye ndi Mulungu, sazatantha ali yense kuti amkonde ndi kum'mvera pakuti ici sicizabweretsa chikondi cheni-cheni kukamkhutiritsa lye.

Tiyenera kupanga chomukonda lye ndipo tidzapempha thandizo lake ndipo azayankha.

Ndiri ndidanga kuti Mulungu afuna kundionetsa m'mene mtima wanga ungaciritsidwe ndi momwe angandisewenzetsere. Ndipo ndimvera wodalirika pondiitana kudzera mu uneneri zaka makumi awiri zapita kugwira dzanja pamene lye acita milakuli. Ndikaika ngati ndinazikhutula kwa Mulungu ndipo ngati sanaitane wopandukira sikunaoneka.

Ndilemba zopitazi kukalimbikitsa kuti mukapitemo mofafana kusandulizika kwa mtima kumene Atate Mulungu anandipasa ndipo ndinacita konse mu Afilika kumene utumiki wathu uli. Manambala ndi mphamvu yake ikukalabe.

Utumiki waukulu pansu pano unapeleka lipoti mu January 2012, muyeso waukulu wachitsitsimuso ciri mkupita patsogolo m'malo eni-eni momwe, tinapereka mabaibulo kumene zaka 35 zapitazo. Lipoti yao ikusonyeza Asilamu ozipereka akulalikira chikhululukiro, chikumasulira zimene malipoti aliri. Asilamu akulandira machiritso a mitima wobvulazika kudzera m'kukhulukira aja owakhumudwitsa, abambo a kufuna kuuza ena cifukwa ndicodabwitsa zomwe ziwaphweteka. Mulungu atha lye ukwaniritsa kupereka monga mabaibulo (ABT), siatumwi cabe oyamba koma akubweretsa gulu lalikulu la m'mbadwo wa a mishonale, Asilamu m'mbiri ya ciyambi wokathandiza anthu awo mwa ubwino.

Chaputala ca 11, chitandiza inu ndi kulankhula ndi Mulungu ngakhale ziyenera kuchokera ku mtima wake. Conde mvetsani kuti azacita cimene mupempha lye cifukwa ciri m'njira ndi cifuniro cake pa inu kubwera pafupi ndi lye.

#### 4. CHIMENE TIRI

Kumvetsa bwino za phunziro la “kuchiza mtima wobvulazidwa“ ndi bwino choyamba kuganzira kuti ndife ndani kuyambira mu buku la Genesis 1:26-28. Timawerenga kuti, “ **ndipo anati, Mulungu tipange munthu m’chifanizo chathu , munga mwa chikhalidwe chathu; alamulire pa msomba za m’nyanja ndi pa mbalame za m’mlengalenga ndi pa ng’ombe, ndi pa dziko lonse lapansi ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi .Mulungu ndipo adalenga munthu m’cifanizo cake, mcifanizo ca Mulungu adamlenga iye: adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane,Muchuruke,mudzaze dziko lapansi, muligonjetse : mulamulire pa nsomba za m’nyanja, ndi pa mbalame za m’lengalenga ndi pa zamoyo zonse, zakukwawa padziko lapansi.” Tsono ife anthu timafanana ndi Mulungu; Iye ndi Mzimu, ndiponso ife tidakhala Mzimu; **“Lifedwe thupi la chibadwidwe, liukitsidwa thupi lauzimu. Ngati pali thupi la chibadwidwe palinso lauzimu.”** 1 Akorinto15:44. Tsono ndizodziwikilatu kuti ndife opambana m’chilengedwe cha Mulungu.**

Koma m’chifukwa chiyani Mulungu adatilenga? Mawu a Mulungu amati, tidalengedwa m’chisangalalo ndi m’chimwemwe chake tsono Adamu asadachite kusamvera Atate ake adali olungama ndi om’kondweretsa Mulungu.Genesis 2 limafotokoza momveka bwino za chisangalalo cha Mulungu pa kulumikizana kwake ndi Adamu tsiku ndi tsiku. Ndipo Mulungu atatha Kumulenga munthu, Mulungu adamukonzera munthu malo odabwitsa osangalatsa osati malo wamba koma munda okongola kwambiri, namuyika iye m’menemo kuti aulime ndi kuyang’anira. Mfumu Davide adamvetsa bwino pamene adalemba Masalimo 8:3-9, **“pakuona ine thambo la kumwamba lanu, ntchito ya manja**

anu, mwezi ndi nyenyezi, zimene munazikhazika, munthu ndani kuti mum'kumbukire? Ndi mwana wa munthu kuti muceze naye? Pakuti munamcepsa pang'ono ndi Mulungu munambveka iye korona wa ulemerero ndi ulemu. Munamcititsa ufumu pa ntchito za manja anu; Mudagonjetsa zonse pansu pa mapazi ace; Nkhosa ndi ng'ombe zonsezo, Ndi nyama za kuthengo zomwe, Mbalame za m'mlengalenga ndi nsomba za m'nyanja. Zopita m'njira za m'nyanja. Yehova, Ambuye wathu, Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi.” Izi zikufotokozera bwino chisangalalo cha Mulungu pa ife m'mene Iye Atikondela kwa thunthu, Ana ake amene tiri ulemelero ndi ulemu wake, ndipo Iye atifungatira ife ndi ulemu ndi ulemelero wake. Eliya, ndipo Paulo adachimvetsa chisangalalo cha Mulungu pa ife, ngakhale mchikhalidwe chatu cha uchimo, pamene adalemba m'buku la Aroma 8:31-32, ndipo nditani ndi zinthu izi? **“Ngati Mulungu ali ndi ife adzatikaniza ndani? Iye amene sanatimana Mwana wace wa Iye yekha; koma anampereka cifukwa ca ife tonse; adzalekelanji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?**

Mulungu adali kumuyendela Adamu tsiku ndi tsiku, kumufotokozera m'mene ayenela kukhalira ndi kumusonyeza zakudya. Adamu adamuchenjeza kuti asadye chipatso cha mtengo wa imfa. Pamenepo tsopano tiwona kukhudzidwa kwa Atate pa Adamu amene safanana mwa m'nofu monga Iye ; Ichi ndi chisamaliro kodi? Eya! Ndipo Mulungu adabweretsa nyama zonse kwa Adamu kuti azipatse mayina. M'mene Adamu adafunira kuti zikhale kuti nyamazo zidakhala. Mwina akhale ndi mzace dzina lina liri lonse Adamu apeleka zonse zimene Adamu adauzidwa ndi Mulungu za m'mene nyama afuna kuti zikhale, Pamene Mulungu adalenga izo chidziwitso cha udindo wake. Mulungu analenga pa pempho la Adamu, kuti iye



akakhutire. Pakutha kuyankha Mulungu, Adamu adadziwa udindo wake, Mulungu afika ku ndondomeko ya gawo **b**, Mulungu am'goneka Adamu ndi kum'chotsa nthiti, namupangira mzake kuchokera ku limodzi la gawo lathupi lake. Ndipo Adamu adadzuka ndi kukondwa ndi mphatso ya mtengo wapatali yomwe Mulungu adamupatsa, chifukwa tsopano m'nzakeyu ndi gawo leni leni la thupi lake, nditha kumva yankho; **ooh**, tsopano iri ndi fupa la mafupa ndi m'nofu wa m'nofu wanga. Ndipo adzachedwa mkazi chifukwa anamtega mwa mwamuna ndi Mulungu osamalira motani yemwe tiri naye. Sitingakhaleenso china kuposa chipatso chadiso lake.

Koma ndiri odabwa chifukwa chimene Mulungu adayikira mtengo oyipawu m'munda wa Edeni. Adamu sakadadya chipatso chake, chikadakhala kuti sichinali m'menemo? Ndipo ndidazindikira chidwi ndi njala yomwe Atate athu ali nayo kwa ife, pofuna kuona kudziyeleka kwathu kwa thunthu pa chikondi chatu pa lye kuti timukhulupirire kwa thunthu. Kodi chikondi cha Adamu chidali choona nthawi zonse? Kapena adayamba kupeputsa pang'ono pang'no chikondi cha Mulungu? "Ngati mundikonda Ine sungani malamulo anga" Yesu adatero; malamulo anga amene muyenera kuwasunga ali abwino kwa inu, pa kuwasunga akusonyezani m'mene mundikhulupirira Ine, kuti ndikakutsogoloreni mu zabwino zanga. Mfundo imeneyo idali yowonadi kwa Adamu.

Mulungu wathu ndi waulemu, Mulungu amene sazaticakamiza kuti tumumvere; ichi ndi chifukwa chake lye adabzala mitengo ya zipatso zokoma munda wa Edeni, kuti akakwanire m'chikhulupiriro chake, kuti Adamu akamumvere lye mu zinthu zonse; koma Adamu adalephera yesero limenero, ifenso talephera. Atate Mulungu wathu amafuna nthawi zonse kuti tumumvere chifukwa nthawi zonse adzatitsogolera kuzofuna zathu. Koma kusamvera lye kumasonyeza Mulungu wathu kuti

sitimukhulupilira Iye. Chonseco Atate athu akupitilizabe kukhulupirira kuti tsiku lomwe ife tidzamukhulupilire mwatunthu potitsogolera m`chiri chonse ndi mzimu wake woyera ku zinthu za bwino zathu, zingabvute maka. Kodi ichi ndi chifukwa chake Mulungu adamuyesera Abrahamu kuti apereke nsembe mwana wake yekhayo **Isaki**; kuti akaone ngati Abrahamu akanamukhulupirira mwa tunthu?

Kodi ifeyo? tsiku lina mtsogolo tingadzafune kutaya miyoyo yathu chifukwa cha Mulungu ndi kuyembekeza Iye kutipatsa zinthu zake zabwino? Zidzakhala choncho, pokha-pokha chikhaliidwe cha Yesu chikadzaumbidwa mwa ife.

Atate Mulungu, adagwiritsa ntchito atate ndi amayi athu adziko lapansi kutilenga ife. Koma Mulungu ndi Atate wathu wona. Makolo athu a padziko lapansi sanatidziwe kuti ndife mwamuna kapena mkazi tisanabadwe, koma Mulungu adatidziwa ife asanatilenge m`mimba mwa amayi, adatiyika kuti chomwe tiri pa miyoyo yathu, Yeremiya 1:5. Ndikhulupilira kuti mbali yofunika ya chilengedwe chatu ndi Mulungu imachitika pa lingaliro nthawi yomwe mzimu wathu umaikidwa m`dzira la m`chibelekeru. Tiri ndi DNA ya Mulungu Atate wathu, ya mzimu, Tidalengedwa kuti tikakonde ndi kukondedwa, monga Iye akonda nayenso afuna kukondedwa. Adatilenga ife m`chimwemwe ndi chisangalalo chake, monga chimodzi-modzi banja limafunira kukhala ndi mwana m`chimwemwe ndi m`chisangalalo chawo, kukhala ndi mwana wokhulupirika ndi chinthu chapadera.

## 5. CHIKHALIDWE CHATHU CHENI-CHENI CHA UCHIMO

Kodi chikhalidwe canga chauchimo chimatanthauzidwa pa kuzimva kuti ndine ofunika kwambiri pa chilengedwe? Kodi ndidakhala ndi kuthekera kotenga chikhalidwe cha mdani wa mkulu wa Mulungu amene akuyesetsa kupitilizabe kutinyenga ife? Mulungu adati kwa iye m`buku la Yesaya 14:12-14, **“Wagwadi kucokeza kumwamba, iwe nthaka, mwana wa mbandakuca! Wagwetsedwadi pansu, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako, ndidzakwela kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wachifumu pa mwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pa mwamba pa phiri la khamu; m`malekezere a kumpoto; ndidzakwera pa mwamba pa mitambo; ndidzafanana ndi wa m`mwambamwamba.”**

Kodi timayeselanso kudzikweza tokha pamwamba pa ena, ngakhale kuti chili chinthu chopanda nzeru? Chifukwa m`modzi yemwe adatilenga ayenela kupatsidwa ulemu monga ali yekhayo ofunika kwambiri. Tinalengedwa ndi DNA ya Atate athu mwa chikondi ndipo kuti tikakhale okondedwa, koma chimo latisokoneza ife koyipa kwambiri motere:

- Mulungu wathu safuna ulemelero wake omwe ngakhale kuti ayenera
- Kutero.
- Ife nthawi zonse tiri odzitanaganidwitsa kuyesetsa kusangalatsa anthu ena kuti akhale osilirika.
- “INDE” safunikiraso kudzitsimikizira yekha. Nthawi zonse timayesetsa kudzionetsera mwakuthekera kwathu. Zachidziwikire, chiri chonse chomwe timachita pa thokha posafunsa kwa Atate Mulungu wathu kuti atichitire;

timamuuza kuti tithe kuchita patokha ndikuti sitifunikiraso thandizo Lake.

- Mulungu amadziwa kutikulenga anthu ndi zinthu zokongola, ayenela kukonda ndikusamalira. Amatitsogolera monga wa ntchito wa luntha, ndi m'busa yekhayo wabwino pa chikhalidwe chatu cha uchimo, sindifenso atsogoleri; timafulumira pofuna kudzipulumutsa tokha; koma talephera ngakhale kulipira ndalama kwa anthu komanso talephera kudzipulumutsa.
- Mulungu safunikanso kukhala pa mpando wachifumu ngakhale kuti amakhala chifukwa ndi mwini zonse. Timakonda kukhala olamulira ena, ndikukhala bwana ndi kuwalamulira. Chifukwa ife, monga ophunzira a Yesu, timatsutsana kuti, wamkulu ndani mu Ufumu wa Mulungu? M'chifukwa chiyani timafuna kuchita zinthu monga mwauchidakwa? Kodi ndidzachichita ichi m'njira yandekha? Tikuyenera kukula pofunafuna Atate athu atiphunzitse m'mene tingapangire zinthu. Mzimu wathu ufunika kuchizidwa ku chikhalidwe chodziyeneleza kuti ukathe kumphunzira kufunafuna Mulungu ndi mtima wonse, pakudzipereka kwa Mulengi Atate athu chifukwa cha chimwemwe chake ndi ulemelero wake pa ife, ndi kukhalanso monga m'mene Ali, ngakhale ndi Mulungu ndipo ife ndi eni ake . Moyo wathu ufunefune kuphunzira kudzipereka ku mzimu wathu ndi kukhala osinthika ndi kumaganiza monga Mulungu amaganizira, 2 Akorinto 3:18, **“Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m`cithunzithunzi comweco kucokera ku ulemerero kumka ku ulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu.”**

Eya, tifunika kusintha ndikuoneka monga Mulungu wathu kachikena mongaso Adamu adaoneka chimodzi modzi monga Mulungu asanachimwe iye.

Mulungu atiuza kuchokera m`buku la Aroma 8:14.... **“Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu.”** Tiyeni tigwire dzanja lake ndi kutsogozedwa ndi Iye; amakonda zimenezo! Ndipo chimenecho ndicho chikondi, mogwirizana chimwemwe, mtendere ndi chisangalalo zizadzala m`moyo wake ndi miyoyo yathu.

Chikondi sichingakhale pamodzi ndikulamulira; chikondi chimafunika kudzichepetsa, chikondi chimatipanga kusaziganizira mwakuzikweza tokha, chimatipatsa khumbo ya kudzipeleka kwa wina ndi mzake ndi kupatsa ena ufulu wopanga zisankho za iwo wokha. Kodi timazindikira kuti Mulungu Atate athu ndi mphamvu komanso ukulu wawo satikakamiza ife kuchita chiri chonse, kodi si Mulungu wodzichepetsa modabwitsa? Adazipanga mowonekela pamene Yesu adagwada panso pamaso pa ophunzira ake ndi kutsuka mapazi a ophunzira pamene kudali kofunika kutero, koma palibe mwa ophunzira ndi m`modzi yemwe akanachichita ichi, adatsimikiziranso kwambiri pa nthawi yomwe adapeleka moyo wake pa mtanda chifukwa cha ife: Chikondi sichingakhale popanda kudzichepetsa ndi kudzipeleka. Kodi mkwati yemwe akonda modabwitsa mkwatibwi wake, sangampatse mphete ya mtengo wapatali yomwe angathe; imene iyesa mulingo wa chikondi chake kwa Iye? Kodi kutumikira kopeleka katundu kwa wina sizionetsa mulingo wa chikondi?

M'mene ife tiwakondera? Atate Mulungu wathu, Mlengi wa zolengedwa zonse, Amadziwa kuti, alandira chikondi kuchokera kwa ife, Iye ayenera kukondanso ife. Koma chifukwa cha chikhalidwe chatu cha uchimo timadzikonda tokha choyamba, ndi kudzikweza tokha pakati pa anthu ena, chifukwa cha ichi sitingapeze zomwe tikhumba ndi kuzifuna, kuti tikakonedwe oooo! Ndife anthu osowekera kwambiri zofuna zathu, timazinamiza tokha ndi kudziwononga.

Mulungu wathu sali choncho, Iye amafuna ubale wa chikondi wokula pakati pa Iye ndi ife, ichi ndi chifukwa chimene adatilengera ife. Izi zitha kutheka pokha-pokha ngati ife anthu tonse tioneke ofunika mofanana, izi zifunikira wumunthu wathu ndi wa Mulungu wathu ngakhale kuti Iye Ali ndimphavu zonse. Chifukwa choti amatikonda ife, mwa chimwemwe chake adzatipasa mwayi woti tipindule m'mphamvu zake tikungoyenera kumupempha Iye. Koma sitingapemphe kolakwika, koma tikhala ndi malingaliro monga Ake, mphamvu ziyenera kugwiritsidwa ntchito pa cholinga chakutidzala m'chikondi chake. Paulo adali odzodzedwa pamene adalemba za chikondi pa 1 Akorinto 13:4-8, **“chikondi chikhale cilezere, ciri cokoma mtima sicutidwa, chikondi sicutidwa, kudzitamanda, sicutidzika, sicutita zosayenera, sicutisata za mwini yekha, sicutipsa mtima, sicutilingalira zoipa, sicutikondwera ndichinyengo, koma cikondwera ndi coonadi, cikwirira zinthu zonse, ciyembekezera zinthu zonse, cipilira zinthu zonse, chikondi sichitha nthawi zonse, koma kapena zonenera zidzakhala cabe, kapena malilime adzaleka, kapena nzeru idzakhala cabe.”**

Kupilira mu zinthu zonse? Hmmm. Ndipo m' buku la 1 Yohane 4:18, **“mulibe mantha m'cikondi koma cinthu cikhala cangwiro kuti citaya kunja mantha, popeza mantha ali naco cilango ndipo wamanthayo sakhala wangwiro m'cikondi.”**

Tikuyenera kukondedwa kuti tikhale, ichinso ndi chimene Mulungu Atate wathu amafunafuna kutchokera kwa ife. Yesu akanapelekanso mtunduwu wachikondi kwa Atate ake, ngakhale adali mu ululu waukulu m'Getsemani, komanotu adasankha kuchita chifuniro cha Atate ake adakhala chimene adaphunzitsa ophunzira ake: ngati mundikonda Ine sungani malamulo anga. Adamu adalephera ku yesero iri ndikuchita kusamvera Atate ake, ifenso timachita kusamvera chimodzi-

modzi, koma Yesu adayima ndi kugonjetsa mayesero. Anamukanso kaciwiri napemphera nati Atate wanga, ngati ici sicingandipitilire koma ndimwere ici, kufuna kwanu kuchitidwe, Mateyu 26:42, ici ndi cifukwa cha Yesu akuchedwa kuti Adamu otsiriza chifukwa adatsirizira kusungabe kumvera Atate ake pa mtengo uli wonse, ndipo adakhala opambana opanda chilema mwana wa nkhosa wa Mulungu amene adachotsa machimo adziko la pansi. Cimenecho ndicho chikondi, ndi ulemu odabwitsa otani omwe Atate ake adamubwezera? **“Ndipo tsopano Atate Inu lemekezani Ine ndi Inu nokha lisanakhale dziko lapansi”**, Yohane 17:5.

Tsopano tiyeni tikambe za zotsatira za chikhalidwe chatu cha uchimo. Kukanidwa kumadza nthawi zonse kwa ife pamene wina adzikweza yekha pa maso panu kapena panga. Kukanidwa kwambiri kumakhala kochepe pamene kwa ena kumakhala kopweteka modabwitsa. Koma chonde kumbukani pamene tidutsa mkukanidwa mwazi ndi thupi ndiye kuti sizikumenyera nkondo ife. Koma tikuthana ndi mphamvu za uzimu mugawo la uzimu kukanidwa monganso chikondi chikhalidwe chazimu pamene takanidwa nthawi zonse ziri m’dzanja la satana lomwe limagwiritsidwa munthu wina kuti atiphweteke tiyembekeze tidzachita owawidwa kudzera kwa munthuyo, ndikuyamba kuvulaza ena munjira yomweyonso mukawona, mtima wa munthu olakwiridwa sudzaonongeka ngati olakwiridwa adzakhululuka omuzunzawo. Ngakhale m’chikhalidwe chatu cha uchimo, satana adzatiletsa kuti tikhululukire otilakwira, ndipo kuwawidwa mtima kwathu kochokera kwa otilakwira kudzayamba kukula mwa ife. Zilonda za uzimu wathu, thupi lathu la umunthu; ngati sizinasukidwe kupopeledwa mankhwala, natsekedwa, kuthandizidwa ndi mankhwala ndi kudzitsuka kuti zikhale zoyera zidzayamba kununkha ndi kukula pakupita kwa nthawi, ndipo zizadzetsa

imfa zilondazo. Ichi ndi chifukwa chake mabanja ambiri amatha atakhala zaka zambiri. Tidziphunzira kukaniza mphamvu ya ziwanda kulowa mwa lfe, pakutsutsana ndi maudani a mtundu uliwonse ngakhale atakhala opweteka kwambiri pa kupeleka chifundo ndi chikhulupiliro kwa onse otilakwira mosachedwa tisanayiwale zomwe zatichitkira. Mfumu Davide adalemba m’buku la Masalimo 4:4, khalani ndi mkwiyo ndipo musachimwe, **“nenani mumtima mwanu pakwamwa panu, ndipo mukhale cete.”** Ndipo Paulo adalemba m’buku la Aefeso 4:26-27, **“kwiyani koma musachimwe dzuwa lisanalowe muli cikwiyire ndiponso musampase malo m’dierekezi.”** “Paulo analiona bvutoli momveka bwino pamenenso adalemba m’buku la Aefeso 6:12, **“cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu ndi maulamuliro ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno ndi auzimu a coipa m’zakumwamba.”** Chikondi ndi chikhalidwe cha uzimu chimodzi-modzi ngati mzimu wathu ukhalabe owawidwa ndi wotilakwira, mikangano yochuluka izadzuka. Tidzayenera kuyiwala zomwe zidachitika, ndipo ndinaganiza kuti mkwiyo sudzachoka kuti mzimu wathu sudzasiya kupweteka. Nthawi simachiza mzimu ovulazidwa, ululu ndi kuwawidwa kudzakula ndipo mbali ya mzimu wathu udzalephera kudzitetedzera pa nthawiyi, lolani Atate anu a kumwamba kuti akhale Adokotala wanu. Tsopano timadana ndi munthu yemwe Mulungu Atate wathu amukonda iye amanena Yesu adamufera pamtanda, Timadziyika tokha m’manyado athu, mkangano waukulu ndi Mulungu. Ine amene ndine mwana wake, ndidelanji munthu amene Mulungu amkonda? Yesu adafera pamtanda chifukwa cha munthu olakwira ena. M’chifukwa chake Mulungu amatichenjeza kuchokera m’buku la 1 Petro 1:15-16, **“monga lye wakufuna inu ali oyera mtima, khalani inunso oyera mtima m’makhalidwe anu onse**



**popeza kwalembedwa muzikhala oyera mtima pakuti, Ine ndine oyera mtima.”**

Ngati tikhala ndi mzimu wowawidwa, Mulungu sangatione, Iye amatitembenukira mkutiwonesa msana zikatero timasowekera chitetezo cha Mulungu Atate ku mphamvu za satana. Mbali ya uzimu wathu yowawidwa imasweka, ndipo timakhala ogawanikana, mboni imeneyi, mphamvu za ziwanda zimakulabe pakumvetsera tsopano kwa atate wa mabodza, izi ndizo m’manenedwe akale, umunthu ogawanika ndiko kutanthauza kuti, masiku ano anthu amakamba za kubisala pa chipande. Mzimu umenewo wowawidwa ukumakula mkupita kwa nthawi, udzapangitsa kuti tikhale ena zomwe zidachitika kwa ife (kubwezera choipa).

Zimafanana kwambiri ndi m’mene Yesu adatichenjezera m’buku la Mateyu 7:1-2, **“Musaweruze kuti mungaweruzidwe. Pakuti ndi kuweruza kumene muweruza nako inunso mkaweruzidwa ndipo ndi muyeso umene muyesa nao kudzayesedwa kwa inunso.”** Mu Aroma 2:1, timawerenga momvetsetseka bwino inu opanda mawu owiringula munthu iwe, amene ali yense wakuweruza pakuti m’mene uweruza wina, momwemo udzitsutsa iwe wekha pakuti iwe wakuweruza umachita zomwezo.

Taganizani zomwe zimachitika kwa ife pamene tipitiliza kuweruza ena ndi kuwawidwa nthawi timayamba kukanidwa kaya tiweruza mowawidwa kwambiri kapena pang’ono “mitima yathu ndi nyumba ya Mulungu mwana wake ndi mzimu woyera koma tsopano kukula kwa mphamvu ya ziwanda imakula pa kudza kwa nthawi imayamba kukwiya, eya ngakhalenso mwankhaza, ndipo zimakulira-kulirakabe mobvuta, kapena kosathekanso kumvera Mulungu ndipo kuti usanjikidwe ndi Mzimu Woyera **Aroma 8:14**, pakuti onse amene atsogozedwa

ndi mzimu wa Mulungu amenewo ali ana a Mulungu. Ichi ndi chifukwa chake akonda am'ndende, amati akatulutsidwe nakalakwanso pakuti amapitirizabe kuchitira ena zomwe ena adawachitira chifukwa samakhululukira. Temberero limenero limatha pokha-pokha ngati mbali yosweka ya uzimu wawo ikhululukira munthu amene adawachimwira, m'mbuyomu ndi kuyamba kuwakonda.

Izi ndi zotsatira za nkondo ya uzimu pakati pa Mulungu ndi satana. Satana amafuna kuti ayiwaritse zomwe zidachitika ndi cholinga choti tikhale osazindikira za kugawidwa kwa mzimu kuti azigwiritse ntchito pa nthawi yake. Utumiki wa Kilementi adachenjeza za mitima yobisika yobvulazidwa m'buku la Ahebri 12:14-15, Londolani mtendere ndi anthu onse, ndi ciyeretso cimene akapanda ici, palibe m'modzi adzaona Ambuye, ndi kuyang'anira kuti pangakhale wina wakuperewera cisomo ca Mulungu, kuti ungaphuke muzu wina wa kuwawa mtima ungabvute inu, ndipo aunyinji angadetsedwe nawo.

Tikayiwala, timataya mwayi wa kupempha Atate chikhululuko pa kupwetekedwa komwe timakhala ndi otilakwira. Ndiponso timazinyenga m'mtima yathu kwambiri kuti ziri bwino ndi ife koma kuvulazidwa kobisika kwa m'kati mwa mtima wathu, tikapitiriza kuchitira ena zoipa pa zimene adachitira. Ndiye kuti tikuzinyenga tokha . Yeremiya 17:9-10, **“mtima ndiwo onyenga koposa ndi osachiritsika ndani angathe kuwudziwa? Ine Yehova ndisanthula mtima, ndiyesa imso kuti ndimpase munthu yense monga mwa njira zace, monga zipatso za ntchito zace.”** Mawu a Yesu adzachita monga tiwachitira enanso, pakuwaweruzwa lwo otilakwira, chimapanga mwamtheradi muzimu. M'buku la Miyambo 28:25-26, **“Wodukidwa mtima aputa mikangano; koma okhulupirira Yehova adzakula, okhulupilira mtima**

**wacewace ali opusa koma oyenda mwanzeru adzapulumuka.”**

Mwachidule kungobwereza zomwe zakambidwa pamwamba apa: Ngati sitikhulukira anthu omwe adatilakwira ife nthawi zonse, tidzakhala tikungoyiwala, ndipo zimakhala zobvuta kuti tikaononge mitima yathu. Satana tsopano mosayembekezera adzagawa mitima yathu ndicholinga chofuna kutiononga.

Ndiri ndi zinthu zambiri zomwe zidandichitikira zina mwa izi, ndipo pamene ndikulemba, ndiri ndi chisoni mtima mwanga, pakuganizira kawiri kawiri osati mosadziwa koma modziwa ndithu, kulakwira anthu m'moyo mwanga. Mwamwayi ndipamene Mulungu wanga mwachifundo ndi mwachisomo adandiombola, kuchimo ya kubvulazidwa kwa mtima wanga, zomwe tsopano nditha kukonda **ndikulemba kuti zikuthandizeni inu.**

## 6. MPHUNZIRO LA UZIMU LA MIYOYO

### YADZIKO LAPANSI

Linayamba pamene Mlengi wathu ayika mzimu wathu m'mimba mwa amayi athu Asanayambe kutipanga ife. Yeremiya 1:5, limati... **“ndisanakulenge iwe ndinakudziwa, ndipo usanabadwe ndikupatula iwe, ndinakuyika kuti ukhale m'neneri wa amitundu ya anthu.”** Mulungu adatidziwa maina athu pachiyambi penipeni, kufuna kuti tiukhale ndi kukhala anthu amene adzamkonda lye ndi mitima yawo yonse, kuti lye ndi ife tikasangalare mchiyangano cha wina ndi mzake nakhala a chimwemwe kwa muyaya. Zikumveka ngati nthabwala sichoncho? Chabwino, ndikhulupilira kuti nthano zinayamba kale pakuti anthu akugwiritsidwa ntchito kuti iwo ndi ife pakukhala ndi khumbo losiyana, pakudikira kubwera kwa Mfumu yathu kupukuta mapazi athu. Mulungu Adapukuta mapazi a Adamu izi ndi zimene Mulungu adaganiza asanalenge dziko lapansi, Timazifunabe zimenezi , chifukwa tinalengedwa mchifaniziro chake , ndimakumbukira bwino-bwino m'mene monga m'nyamata wang'ono nthawi zonse ndimalira ndikamva nthanoyi, ndipo adakhala achimwemwe mpaka kale,” Eya, ndizimenenso ndikhala ndikudikhira, ndipo mukudziwa inu? Atate athu ali ndi mfumu yomwe ikudikira kwa nthawi yaitali, koma adziwa m'mene ukwati udzachitikire.

Chibvumbulutso 22: 13 – 17 Chimati: Ine ndine Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza. Ciyambi ndi Citsiridziro, odala iwo amene atsuka mwinjiro yawo kuti akhale nawo ulamuliro pa mtengo wa moyo kuti akalowe ku mzinda pa zipata. Kunja kuli agalu ndi anyanga ndi achigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano ndi onse okonda bodza ndi kulichita. Ine Yesu ndituma m'ngelo wanga kukuchitirani umboni za izi m'mipingo. Ine ndine muzu ndi mbadwa ya Davide. Nyenyezi yonyezimira ya mbanda

kucha. Ndipo Mzimu ndi Mkwatibwi anena, Idzani ndipo wakumvera anene adze iye wofuna atenge madzi a moyo kwaulere. Ndipo buku la Aefeso 5: 25 -26, likuti, **“Amuna inu kondani akazi anu monganso khristu anakonda Eklesia nadzipereka yekha m’ malo mwace. Kuti kumpatula amyeretsa ndi kumsambitsa madzi ndi mau.”** Pamene ndiyendetsa galimoto mu Afilika mu utumiki oyenda kapena kuyendera ndende, zosangalatsa kwambiri m’maulendo anga ndi ana achichepere amene athamangira kum’sewu. Ndisanawafikire iwo ndimatsitsa madzenera agalimoto kuti ndikawayankhe manja awo akupizidwa ndi nkhope zawo za chimwemwe. Amakhala odzazidwa ndi chikondi, ndikukhala ndi chidwi choyandikira pafupi ndi ine. ndipo ndikawabwezera kukupiza dzanja langa ndi nkhope ya chimwemwe amakondwera kwambiri .

Nthawi ndikuwazindikira, kugwirana nawo chanza ndi kuliza zala zanga pa mutu wa mwana, ndipo winanso amadza pafupi nafunanso kuti ndimupange chimodzi-modzi. Chikondi cha pelekedwe ndi mosavuta ndi anawa a chichepere ndikulandilidwa ndi iwo. Kodi amakupiza manja awo kwa odutsa chifukwa ali ndi chikondi chochuluka kuposa chikondi chomwe mai wawo amawapatsa? Kapena chifukwa cha umphawi omwe miyoyo yawo imadutsamo? Ngakhale ophunzira a Yesu, pamene adabweretsedwa kwa lye timawerenga izi m’buku la Mateyu 19:13-15, **“pamenepo adza nato tiana kwa lye, kuti aike manja ake pa ito ndi kupempherera, koma ophunzira amawadzudzula, koma Yesu anati tilekeni tiana musatikanize kudza kwa lne, chifukwa ufumu wakumwamba uli wa wotere ndipo lye anaika manja ake pa ito, nachokapo.”** Muzindikira m’mene akulu-akulu akhumudwira ndi ana, koma Yesu sali choncho. Anthu amene

ali ndi mitima yobvulazidwa samafuna kuonetsera kapena kupeleka chikondi chachikulu.

Sindimamvetsa kuti ndi chifukwa chiyani ndime yaciwiri ya Masalimo 8 inayikidwa, yomwe imaoneka kuti ndiyovuta kumvetsa: limenero ndirimene lidali bvuto langa, tiyeni tiwerengwe gawo loyamba la masalimo 8, **“Yehova, Ambuye wathu, Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi! Inu amene mudaika ulemelero wanu pa thambo la kumwamba. Mkamwa mwa makanda ndi oyamwa mumakhazikitsa mphamvu chifukwa cha otsutsana ndi inu kuti muwaletse mdani ndi kubwezera chilango pakuona ine thambo la kumwamba lanu, ntchito ya zala zanu mwezi ndi nyenyezi, zimene munazikhazikitsa, munthu ndani kuti munkumbukira? Ndi mwana wa munthu kuti mucheze naye? Pakuti munamchepa pang’ono ndi Mulungu munamveka lye korona wa ulemelero ndi ulemu Davide anadabwitsidwa kuti Mulungu asamalira kwambiri umunthu pakutiganizira, kutiyendela, kutifungatira.”** pamenenso nthawi yomweyi akutitenga kukhala adani ake kutengera pa vesi 2 Davide adamvetsetsa momwe Mulungu wathu amalandilira chikondi chodabwitsa ndi mphamvu zambiri kuchokera kwa ana, pamene mwachidziwikire akutenga akulu akulu kutchulidwa pamodzi ndi satana, pa kusasamala za Mlengi. Dzina la Mlengi ndi lopambana kwambiri pa dziko lonse lapansi, chonsecho, timadzikonda tokha kuposa lye kapena kuposa wina aliyense mwina timankanira limodzi Mulungu, chonsecho Mlengi sasiyabe kusamalira ndi kutiyendela. Kodi mukumbuka? Adamu ndi Eva anadzimverera pamene Mulungu adauza njoka kuti mbewu ya Eva idzapwanya mutu wa mbewu ya njoka ndipo idzalalira chidendele cha mbewu ya Eva, kumgonjetsa satana kwa ife, Atate athu sasiyabe kutiganizira. **Zikomo Atate!**

Tikhoza kutengera makhalidwe abwino kuchokera kwa makolo athu amene adatisiya kale, komanso makhalidwe oipa, chimodzi modzinso m'badwo wa Adamu ndi Eva anatengera chikhalidwe cha uchimo kuchokera kwa Adamu. Chifukwa cha chikhalidwe cha uchimo tadzazidwa ndi upandu, kuganiza kuti palibenso amene atha kudalilidwa kuti angatisamale kuposa kudzisamala tokha, mongaso Adamu adachita kusamvera kwa Atate wa chikondi chodabwitsa ndi okhulupilika wa mphamvu zonse. Ifenso kawiri-kawiri timamukana ndikungoganizira zofuna ndi zokhumba zathu zokha zofunika kwambiri kungofuna kukonedwa basi. Ndife odzazidwa ndi kuzikonda ndi kumaganiza kuti anzathu akutipondeleza kuti tipeze zofuna zathu ndipo timakhala wopikisano wina ndi mzake, ndipo nthawi zina ndi kumavulazana tokha. Tataya masomphenya akuti, ife tikonedwa, tikuyenera kukondanso kupeleka munthu amene akonda kwambiri amaperekanso kwambiri, ndiye kapolo wamkulu kwambiri pakukwaniritsa kumva kuwawa kwambiri timasankha kukhala mabwana a anthu ena, ndi kukana anthu ena zimachitikira m'moyo, izi zimachulukira koposa chikondi. Kukanidwa kumachitikira tonse ndipo munjira zosiyana-siyana kutigwetsa pansu, wina, kutibela, kutinamiza, kutinyoza pagulu, kutizunza nthawi zina zambiri. Ndipo chikhalidwe chatu cha uchimo chipangitsa kusakhulukira anthu otalakwira, koma kuyesa kuiwala zomwe zidachitika ndipamene kuwawidwa kumakulira- kulira ndi Kuzunzidwa kwa mtima. Kenaka timayamba kudziteteza tokha, kum'chitidwe wodzivulaza pa kudzipatula pa anthu azanthu kapena kutalikana nawo, tikatero timatalikanso ndi Mulungu. Tikunikira chikondi kuti tikhale achimwemwe ndi athanzi koma tapangitsa chikondi kuti chitalikire. Ndipo ngati sitingakonde anthu ena sitingakondeso Mulungu wathu. Mphunziro la moyo, bvuto ili lidzakula kwambiri, mwachiyembekezo. Tsiku lidzafika pamene chozizwa chidzafika ndikuona kuti tiyenera kubwerera ndikupempha

chikhululukiro kuchokera kwa Mulungu chifukwa chakuweruza konse komwe tidachitira anthu ena m'malo mwake ndikuyamba kukonda, ndikukululukira anthu omwe sadatilakwira m'njira ina ili yonse

Timakwiya mwachangu, eya ndikukhala owawidwa ndi wina aliyense amene sanatilemekeze, watizunza ndi kutivulaza ndipo timaganiza zopeleka chilango posamukhulukira. Koma mwakusadziwa kuti tikuzipweteka tokha.

Muli monse, taganizirani chikhalidwe cha Mulungu ndi chikondi amafuna ubwenzi wa pamtima ndi ake onse ndipo akuyetsa kuchita cina ciri conse kuti atisendeza pafupi ndi Iye. Amatikondanso kwambiri, adatipatsa mwana wake kuzasenza chilango cha machimo athu, makhalidwe athu amafano kuti ngati tikufuna tisendele pafupi naye, titha, koma ngati tisankha kupitirizabe kudana ndi adani ambuyo mwake. Timaziika mkusemphana kwakukulu ndi Mulungu. Yesu adafotokoza mbuku la Mateyu 18: 32-34, Pamene akunena za fanizo la kapolo osakululukira amene amakhulukidwa ngongole yake kuti tisabweza. Komano afunitsitsa kuti wina amubwezere ngongole yomwe adatenga kwa iye ngakhale kuti sakanatha kubweza. Ndipo Mbuye wake anati kwa iye: kapolo iwe woipa, ndinakhulukira iwe mangawa onse aja momwe muja unandipempha Ine. Kodi iwe sukadam'citira kapolo mzako cisoni? Ndipo Mbuye wake anakwiya, nampereka kwa azunzi, kufikira akabwezere iye mangawa onse. Kodi mukudziwa kuti Mulungu adzaletsa satana kutinyenga pamene tiyenda ndi Mulungu? Koma ngati tidzikaniza tokha kuyenda naye. Atate athu akumwamba adzatichokera m'moyo wathu, ndipo kumapeto ake tidzagwa m'mapazi a satana ndi ntchito zake. Gawo lija la mzimu wathu limayamba kukhala pansu pa ulamuliro wa satana. Gawo lathu lakuweruza ena mobwereza-bwereza. Nthawi zambiri titha kulephera kudziwetsa pamene



kuwawidwa kwa mkati mwathu kukula-kulabe zikhoza kudzetsa kuzunzidwa kwa uzimu mkati mwa mtima wathu. Ndinakakhala otero moyo wanga kwa nthawi yaitali. Timagwa munyengo zomwe zimasintha zinthu m'nthawi yaitali kapena yaifupi. Mkuganiza kwa umunthu, nyengo zotere ziri ndi mayina osiyasiyana kumabvuto amitundu mitundu. Ndadutsa muzinthu zambiri. Ziwanda zochuluka zokhala mtima mwa munthu, maluso amene Yesu ndi Mzimu Oyera amakhalamo, zimakhala zinthu zobvuta kuzimva ndi kutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Aroma 8:13-16 limati: **“pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi; mudzafa; ngati ndi mzimu mufetsa zocita zace za thupi mudzakhala ndi moyo. Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu amenewo ali ana Mulungu. Pakuti inu simunalandire Mzimu wa ukapolo kucitanso mantha; komano munandira umene timafuula nawo kuti Abba, Atate. Mzimu yekha acita umboni ndi Mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu.”** Kodi tsopano mwamvetsa chifukwa chimene sitingabwere chifupi ndi Mulungu pamene tikula?

Choyamba ndikuyakha mowawidwa ku zolakwa zatsopano zomwe zimatifikira, chachiwiri kuwawidwa kuchokera kuzironda zakale zimene sizinapozedwe, zimakulabe mphamvu. Unyinji wa ziwanda, umatipangitsa ife abambo kukwiya msanga nthawi zambiri azimayi kukhala ndi munthu pa zinthu zocheza zopanda pake. Mizimu yoipa yaziwanda imatipangitsa kuti timve ngati sitimawelenga Mau a Mulungu pafupi pafupi pamene takonzeka kuwelenga mau a Mulungu, mwadzi timayamba kugona, timayamba kupemphera pang'ono-pang'ono, kapenanso ikafika nthawi ya kupita ku chalichi, basi timaganiza kuti tayamba kuzizidwa.

Kodi yankho lamabvuto amenewa ndi chiyani? Yesu akutipatsa yankho m' buku la Mateyu 18:3–8, **“Nati Indetu ndinena kwa**

**Iwe, ngati simutembenuke mtima simudzalowa konse mu ufumu wa kumwamba. Cifukwa cake yense amene adzicepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu ufumu wa kumwamba. Ndipo amene adzalandira kamwana kamodzi kotereka cifukwa ca dzina langa, alandira Ine. Koma yense amene adzakhumudwitsa kamodzi ka tiana iti takukhulupirira Ine, iye kuti mphero yaikuru ikolowekedwe m'khosi mwace, namizidwe poya pa panyaja.”**

Sikuti Yesu pano akutiitana kuti tikhalenso tiana monga akulu adzicepetse okha ngati mwana anafunafuna kuchotsedwa moyo wankhaza ndi kuwawidwa kamba ka kusakhululukira. Tsopano tikhale ndi mtima omasuka kuti tisaziteteze tokha, pamene tidziwa coonadi cha mbiri ya miyoyo yathu yopanda ululu chifukwa takhululukira adani athu. Tidakhulukira, ndiponso Mulungu adakuza chikhululukiro chake chimene chimabweretsa mtendere. Mutikhulukire zochimwa zathu monga ife takhululukira amangawa athu. Kodi mumamvetsa Yesu chimene amatanthauza, Adatiitana kuti timutsate. Pakudzikaniza tokha ndi kunyamula mtanda wathu tsiku ndi tsiku. Luke 9:23-25, **“Ndipo Iye ananena kwa onse, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace tsiku ndi tsiku, ananditsate Ine. Pakuti amene afuna kupulumutsa moyo wake iye adzautaya; koma amene aliyense akataya moyo wace chifukwa ca Ine iye adzaupulumutsa uwu. Pakuti munthu apindulanji akapatha dziko lonse lapansi nadzataya moyo wace? Kapena kulipapo moyo wace?”**, kukonda adani athu ndi mbali imodzi yotaya miyoyo yathu, chifukwa ambiri adzati Eya , kukonda anthu tiyenera kumva zowawa zambiri .Yesu akufotokoza bwino m'buku la Mateyu 5:38-39, **“Munamva kunenedwa, kuti diso kulipa diso, dzino kulipa dzino, koma**

**ndinena kwa inu musakanize munthu woipa, koma munthu amene adzakupanda patsaya lako lamanja umutembukire mbali inanso.**”Koma kodi simunthu wathu omwe umakuza chikhululukiro chatu kwa lwo atilakwira ife; ndipo atitsutsa ife? Kodi zirona zathu timathana nazo bwanji mtima mwathu ndi kuganiza za Mulungu Atate athu? Ndidzapemphera kwa Abba adzatipatsa mtima wakupemphera kwa Iye zambiri mu ufumu wake, ndikulimbikitsani mdalitso woyamba wa Yesu womwe adalankhula ku chipunzitsa ca pa Phiri m’buku la Mateyu 5:3, Odala ali Osauka muuzimu chifukwa uli wawo ufumu wa kumwamba.

## 7. MTIMA, MOYO NDI MALO ANKHONDO YA UFUMU WA MULUNGU

Mtima ndi Moyo ali Malo a nkhondo ya Ufumu wa Mulungu ngati sitilandira chikondi, timakhala wokwiya ndi wowawidwa m'moyo, wodwalika ndipo pamapeto pake kufa kuthupi. Ngati Atate athu alandira chikondi chochepa, amafoka, koma ana achichepere atha kumulimbikitsa ndi chikondi chawo. Masalimo 8:2, Izo ndizo satana adziwa, ndipo ichi ndi chifukwa apitilizabe kulimbana ndi Mulungu Atate wathu kuwayesa, pakutichotsa lfe chifupi ndi lye. Anayamba kutiukira kuchokera m'mimba mwa amayi athu. Kodi satana amatiukira motani? Pakutiyanbanitsa pena kutikhumudwitsa, kutipweteka kutizunza ndi zina zambiri. Eya zolakwa zizatifikira tonse ndipo ifenso timalakwira ena, pakuti tonse tinachimwa napelewela mu ulemelero wake. Ndiposo satana amatinyenga kwambiri pakutichititsa ife kuzonda otirakwira, koma osati kuzizonda tokha pakuti nafe timalakwira ena makamaka, satana amagwira ntchito ngati imeneyi yakutiwalitsa machimo akale, zomwe zimakhala zosabvuta tokha kuti ndife abwino kuposa ena ngati sityenda limodzi ndi Mulungu.

Zimadabwitsa mkuona momwe timawaonera akaidi kukhala zigawanga posazona tokha zomwe tachita ndizimene tikupitilizabe kuchita, sititha kuziona izi chifukwa mitima yathu yoipa imabisa choonadi. Tonse tikufunikiradi kwambiri kuwala ndi choonadi kuchokera kwa Mulungu. Yelemiya 17:9-10, **“mtima ndiwo onyenga koposa ndi osachiritsika ndani angathe kuudziwa? Ine Yehova ndisanthula mtima ndiyesa imso, kuti ndimpatse munthu yense monga mwa njira zace monga zipatso za ntchito zake.”** Davide adachimvetsa bwino ichi pamene ananena kuchokera m'buku la Masalimo 51:6, pamene adapha Uriya ndi kukwatira mkazi wake Basheba.

Onani Inu mukondwera ndi zoonadi m'malo a mkatimo. Ndipo m'malo atseri mudzandidziwitsa m'nzeru ndipo Davide adalembaso m'buku la Masalimo 43:3-5, **“Tumizirani kuunika kwanu ndi coonadi canu cinditsogolere, zindifikitse ku phiri lanu loyera, kumene kukhala Inuko kuti ndipite kufikira kuguwa la nsembe la Mulungu. Kufikira Mulungu wa chimwemwe changa ceni-ceni. Ndikuti ndikuyamikeni ndi zeze, Mulungu. Mulungu wanga. Udziweramiranji moyo wanga iwe? Ndi kuzingwa m'kati mwanga? Yembekeza Mulungu; pakuti ndidzayamikanso; ndiye chipulumutso cankhope yanga, ndi Mulungu wanga.”** Zoonadi, maganizo achoka ndi thandizo la Mulungu. Yesaya 61:3, ndikonzere iwo amene alilira maliro m'Zioni ndi kuwapatsa cobvala chokometsa mwa phulusa. Mitima ndi miyoyo ndi malo ankhondo amene satana amenyana ndi mphamvu ya ukulu ndi ufumu wa Mulungu. Kodi timamvetsa momwe nkhondo zimakanthidwira? Kodi timamvetsa chifukwa chimene timakhala ndi khumbo lochepa kusendera chifupi ndi Mulungu? Davide adalemba kale m'buku la Masalimo 14:2-3, **“Yehova m'Mwamba amawelamira pa ana a anthu kuti aone ngati aliko wanzeru, wakufuna Mulungu. Anapatuka onse; pamodzi anabvunda; mtima; palibe wakucita bwino ndi m'modzi yense.”** Kodi tingabweretse bwanji kwa Mulungu wathu ndi mitima yathu ngati ana achichepere? Aaaaah! ngati tingathe kuona momwe nkhondo ya ana a Israyeli inkayendera kukapumira m'malo amalonjezano ndipo mwachangu tinakalowa mu m'mphumulo wa Atate wathu, chilichose ndi chotheka. Mu zonse ndi m'modzi yekhayo wa mphamvu zonse. Thandizo lathu liri m'dzina la Ambuye amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi **Masalimo 124:8,**

Mkusiyana kotani kumene kudafika pamene kapolo m'neneri Elisa pamene Ambuye adatsekura maso kuti aone zoonadi mu

uzimu. Kusiyanana kumene Elisa amaona pamene m'nkhondo mzimu ikucitikira. 2 Mafumu 6:14-23, **“Pamenepo anatumiza akavalo ndi magareta ndi khamu lalikulu, nafikako usiku, nauzinga mudziwo. Ndipo atalawirira mamawa mnyamata wa munthu wa Mulungu, natuluka, Taonani, khamu la nkhondo mudzi ndi akavalo ndi magareta. Ndi mnyamata wake unanena naye, kalanga ine, Mbuye wanga tichitenji nati iye usaope pakuti okhala pamodzi ndi ife acuruka koposa aja okhala pamodzi ndi iwo. Ndipo Elisa anapemphera; nati, Yehova mumtsegulire maso ake kuti aone. Pamenepo, Yehova anamtsegulira maso mnyamata napenya iye, ndipo taonani paphiripo panadzala ndi akavalo ndi magareta amoto akumzinga Elisa atatsikira pali iye, Elisa anapemphera kwa Yehova, nati, mukathe mtundu uwu ucite khungu. Ndipo iye anawakantha nawacitisa khungu, monga mwa mawu a Elisa ndipo Elisa ananena nawo; ngati njira ndi iyi ngati mudzi ndi uwu? Munditsate ine ndidzakufikitsani kwa munthuyo mumufunayo nawatsogolera ku Samariya ndipo kunali pakufika ku Samaria, Elisa anati, Yehova muwakanganure awa maso ao naona iwo, ndipo tapenyani pakati pa Samariya. Niti mfumu ya Israyeli kwa Elisa pakuwaona Atate wanga kodi ndiwakhathe? nati musawakhathe kodi mumakantha omwe mwawagwira ndi lupanga ndi uta wanu? Apatseni mkate ndi madzi adye namwe namuke ambuye wao ndipo anawakonzera cakudya cambiri nadya namwa iwo, nawauza amuke namuka kwa mbuye wao. Ndipo magulu a Aramu sanadzanso kudzikira la Israyeli iyi.”**

Ndi nkhanu ya chitsanzo chachikulu cha zimene Mulungu adachita chifukwa maonedwe auzimu wa Elisa, ndi kukonda adani athu kwa modzala. Ndikupemphera kuti Mulungu Atate atsegulenso maso athu, kuti tione nkhondo zenizeni, zomwe ziri

m'mtima mwathu m'nyumba za mzimu wathu m'miyoyo yathu momwe muli kuthekera kusankha chabwino ndi choipa kusankha Mulungu kapena kumukana lye. Mizimu itha kukhudza kwambiri momwe timamvera tangoganizani ndipo muone ngati simunakumana nazo, mwina mudzathe kutenga nthawi yoyenda mu Afilika, ndiwo umene uli m'chitidwe wakupemphera mumzimu umachitika. Ku dziko kumene mphamvu za ufiti ndi zochuluka komanso ndikumenenso Mulungu amaonetsa mphamvu zake, kumene Mulungu anagonjetsa satana monga afunira pa kuchititsa zodzizwitsa kudera la anthu amene amupempha ndi kumvetsera lye, ku mau ake, ndiponso amabweretsa mtendere ndi moyo wathanzi. Izi mwinanso zitha kukhala zobvuta ndi malingana azungu amene amaona kuti ndi zinthu zosamva kuchita ngakhale osapempha kwa Mulungu chiri chonse. Mukuona ngati anthu ali ndi bvuto nakhulupirira kuti kulidi Mulungu ndipo mdierekezi, satana azikonda izi adzapambana ndi kuwachotsa pamaso pa Mulungu. Ndipo satana amakondwera ndi kuthandiza anthu kupeza zithu zabwino, "m'njira zawo-zawo", kuthandiza maganizo awo kuti safunikiranso thandizo la Mulungu. Kodi ndi chifukwa Mulungu amelekerera m'chitidwe umenewu? ndi chifukwa chiyani Mulungu sazionetsera yekha momveka bwino kuti satana sangate kuchotsa kwa lye? Mulungu amafuna chikondi chathu amakhala ndi khumbo lakuti ife timufunefune ndi mtima yathu yonse ndipo lye ali wopezekeratu m'chilengedwe chake. Koma tikumukanabe lye, Paulo adalemba izi mbuku la Aroma 1: 19-20, "**cifukwa codziwika ca Mulungu caoneka mkati mwao pakuti Mulungu anacionetsera kwa iwo. Pakuti cilengedwere dziko lapansi, zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace: Popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa kuti iwo adzakhale opanda mawu akuwiringula.**" ngati Mulungu adziwonetsera yekha kudziko

losakhulupirika, ikanagwa ndi maondo ake ndi mantha osati ndi chikondi bvuto silakuti Mulungu sangapezeke koma ndi lakuti timamutchukitsa kwambiri satana kapena kumpatsa mpata wambiri opezeka m'mitima mwathu.

Panthawi yotumikira kawiri kawiri ndimafotokozera, Miyambo 3:5-8, kumene Mulungu amalonjeza njira zoongoka zosabisika ngati tichita zonse ndi Iye. **“Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, osacilimikizika pa luntha lako. Mlemekeze m'njira zonse ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako, adzakupambanitsa pomaliza. Tsopano ndizindikira lonjezo la Atate anga tsiku ndi tsiku. Alipo ndipo modziwikiratu apezeka mtima mwanga.”**

Ndi muno mu Afilika m'mene anthu akumtumikira Mulungu kuchokera kumaiko a azungu amakhulupirira mawu a Mulungu modzizwitsa kuti ndi moyo ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zomwe zimachitika patsiku. Zimakhala zosavuta kukhulupirira kuti Mulungu adagawa mamita 2000 kuya kwa Nyanja yofiira kukapulumsa anthu ake pamene anali kulira chifundo chake. Mulungu m'masiku a Gidiyoni adaononga asilikali a Midyani ndi dzanja limodzi pa kukhazikitsa malingaliro a ankhondo kuti akaphane okha wina ndi mzake ndipo amfumu Davide anapha Goliati kuti akathetse m'nyonzo wa Mulungu. Israyeli anakhulupirira Mulungu pa kuombola Israyeli kuti mkatikati mwa unamwilo wa mtundu Yehosafati mu Yudeya, adagonjetsa amuna chikwi chimodzi amphamvu, Amon, m'moabu, msilikali wa Seiri pakumenyana okha okha. Chifukwa, Mulungu adabzala malingaliro awo pakukhulupirira zozizwitsa zomwe Mulungu adachita kudzera kwa m'neneri Eliya ndi Elisa. Adadziwa chimene iwo adali pa uneneri wa Mulungu pa Israyeli pakukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu wamoyo amene adachiza ndi kuukitsa anthu kwa akufa. Adakhazikitsa bata namondwe ndi nyanja, adachita zozizwitsa mopitilizabe



monga adali kutsogozedwa ndi Atate ake adapanga chiyanjano ndi Atate ake ndi Atate athu opezekeratu kwa tonse kudzera nsembe yachitetezo ya pa mtanda miyoyo yatha makhalidwe a mizimu. Nthawi zambiri ankachitika mosadziwika zimene zimapangitsa ife kwambiri kusatetezedwa ku chinyengo ndi kumvetsa bwino Masalimo ndi Miyambo zomalangiza bwino za izi. Chiyambi cha nzeru ndiko kuopa Yehova. Ndichifukwa chiyani kuwopa Yehova kumatipatsa nzeru?

Ziwanda zitha kukhudza malinagaliro athu monganso Mzimu wa Mulungu ndi Angelo koma Mulungu wathu ndi Yekhayo amene Ali ndi Mphamvu zonse amene akhoza kumletsa satana ndi ziwanda zake koma adzachita zimenezo pokha pokha ngati timuwopa ndi kumufunafuna Iye. Satana anakwiya pamene Mulungu anatuma Mwana wake m'dziko lapansi. Adali kufunafuna nthawi zambiri kumletsa Mulungu palonjezo lomwe adacita kwa Adamu ndi Heva pa kuika udani pakati pa mbeu ya satana ndi mbeu ya Heva kuti izapwanyanya satana. Koma mwa ici yesero ina iri yonse idalephera, ndipo Yesu adali okonzeka kuyamba utumiki wake. Tsono, satana adayesa kumletsa Yesu, kumuyesa Iye pamene adasala kudya masiku makumi anai ndipo sadafoka kwambiri. Kumbukani, Yesu adali ndi umunthu, monga inu ndi ine. kusiyana komwe kunalipo ndi kwakuti adali Mwana yekhayo wokondwa wa Atate, ndipo kenako pakanapanda chikhalidwe chathu cha uchimo, akanasankha kusamvera chifuniro ca Atate ake, monga Adamu adasankhira. Munjira ina iri yonse Yesu adali monga ife, sakadatha kuchita china chiri chonse kodabwitsa pa Iye yekha ndipo Yesu ananenetsa kuti: pamenepo Yesu ayankha iwo, indetu, indetu, ndinena kwa inu, sakhoza mwana kuchita kanthu payekha, koma aona cimene Atate acicita ndico. Pakuti zimene Iye azicita, zomwezo mwana azicita momwemo. Yohane 5:19. Tsopano pamene mdierekezi adayesetsa kum'nyenga Yesu ndi

mafunso, Kodi Yesu adayankha bwanji? Adafananitsa pakuona zifukwa zimene satana adamupatsa pa zomwe Mulungu adazilemba m'mbuku. Ifenso tizichita zomwezo nthawi zonse, kuti tikapambanire nkondo zathu za Mulungu wathu. Chitani zonse ndi lye ndipo lye adzaongola njira zanu zonse. Kudziwa mau a Mulungu atha kutisunga ife m'chifuniro chake ngati tifuna. Kodi izi sizodabwitsa Mulungu wathu angatitetezere ife kuzitenga kudutsa m'zinthu zosocheletsa ngati timupemphera zidzakhala choncho, ngati mu ubwezi akhulupirika ndi lye timulola lye kutithandiza pamene tipanga chiganizo ndi Mulungu, Atate wa Ambuye wathu Yesu

## **8. ATATE MULUNGU NDI YESU KRISTU ACHIRITSA**

Kuchiritsidwa kwa zirona m'mitima yobvulazika yidaliro pa mphamvu ya Mulungu. Munthu yemwe ali ndi bvuto lalikulu losakhala ndi anzake Dissociative Identity Disorder (DID)), kale uchedwa kuchuluka kwa makhalidwe osalunjika (Multiple Personalities Disorder (MPD)), angakomane ndi dotolo wa bongo kaya dotolo openya pa openga kuti achiritsidwe, ndipo angathe kuthandiza munthuyu kwa zaka zinai kapena zisanu ndi cimodzi, kumupatsa uphungu kawiri pa sabatha limodzi kwa ola limodzi ndi opengawo angathe kukhala ataima bwino tsopano. Ndiye tsopano opengawa akhalabe obwerera kuzakomana ndi dotolowu kuti apitilize kupereka thandizo; kupereka chiritso kuyetsedwa pa muyeso wa bongo, zinthu zonga zabongo, monga tanthauzo iliri, zingathe ndi mzimu kwatha. Mabvuto onse mumaganizidwe ndi auzimu koposa m'mbongo ai. Masukulu amaphunziro, koma samaphunzitsa aphunzi pa mzimu popeza analoredwa kuphunzitsa cabe pa zimene sayansi inasimikizira. Satana anasokoneza cimango ca maphunziro m'masukulu apamwamba kuti salongosola zophunzitsa cifukwa a sayansi nabwera kukabvomereza ndi kumangiriza "Scientific Conclusion" pa phunziro popanga m'ndanda wa zophunzitsa kubvomereza popanda mzimu. Nthawi iriyonse anthu akapemphera kwa Mulungu kuchokera m'tima wao kupempha chikululukiro pokhalibe wokwiya kwa nthawi itali ndi munthu yemwe anamlakwira ndi kupempha Mulungu awathandize tsopano ayambe kukondanso adani ao, ndiwona kuchiritsidwa bwino kwa zirona muuzimu. Kumvera m'kwiyo ndi kuwawidwa kwa kanthawi koma kubwezera pemphero zirondazo zichiritsidwa. Mulungu azakhulukira ife ndi kuchiritsa zirona nthawi zonse ngati tikhulukira adani athu, kweni-kweni momwe Yesu anaphunzitsira mu pemphero

la Ambuye. Ndiona anthu mu Afilika kubwera kwa Mulungu mwapemphero iyi cifukwa amayankha mofulumira mapemphero ao; ndiye momwe anthu azindikira kuti Mulungu alimoyo.

Mu November 2018, ndinalandira lipoti limene ndanenapo kale m'ciyambi, mkulu wa Asilamu, mtsogoleri wa magulu omvetsera mabaibulo olankhula (ABT) analoweza ndi kusewenzetsa (***Healing Wounds of the Heart***) kuchiritsidwa kwa mtima wobvulazidwa, ziphunzitso zinabweretsa chikondwerero nati! “Sichapafupi inuyo kutitsutsa kuti tilowe m'chikristu, koma momwe zinthu zikuchitikira citengera Mulungu cabe.” Atsogoleri awa apeza ubwino koposa muyeso woyikika kale cifukwa ndi mitima yomasuka ali ofuna kulandira ndi kugwiritsa mau a Mulungu.

Ife anthu, ndife mizimu ndipo zironda za mtima ndi zauzimu m'chirengedwe. Mitima yathu ndi yobvulazikidwa pamene tiweruza ena ndi mkwiyo, amene anatikana ife m'njira iriyonse, koposa kutikonda ife. Chikondi ndinso kukana ndi zauzimu ndipo yankho ya izi ikhalabe mu uzimu. Kuweruza molunda mtima konse kumene tacita, tiyenera kumasula uko, poti Mulungu angatifikatire ife. Yesu anati momveka monga, Mateyo 6:14-15, **“Ngati mukhululukira adani anu zolakwa.”** **“Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zao adzakhululukira inunso Atate wanu wa kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate wanunso sazakhululukira zolakwa zanu.”** Kukana kupezeka kwa Mulungu kaya kumupandukira sikuzapereka yankho ku zironda zanu.

Monga anthu aku Mwera, Aluya akuchotsa ndi kucoka kukakhulupirira Mulungu, sikudzakhala ngakhale tsopano malo konse komwe anthu azapita m'mitima yao yobvulazika ndi ici,

mtendere umene Mulungu angapereke. Mu March 11, 2019, tiona kubwera pansi kukupitiriza, cacisoni kuti anthu sakuphunzira kuchokera kumbiri. Esaya ananenera kale pa kugwa pansi kwa makhalidwe m’masiku ake mu ufumu wa Yuda ndi Yerusalemu’ m’mene amai atenga ulamuliro wa mabanja ndi magulu a anthu achikhalidwe cimodzi. Ngakhale anyamata osamvera anayamba kulamulira zionetsero: Onse cifukwa m’kwiyo ndi kuphwetekedwa kwa mitima, bambo anakhala chibvuto motsatira ndi kumacita citsembwere, kumagonana amuna okha-okha kukhala temberero monga masiku a Sodomu ndi Gomola.

**Tiwerenga Yesaya 3:1-12: “Ndipo onani, Yehova wa makamu wacotsa ku Yerusalemu ndi ku Yuda m’cirikizo wocirikiza cakudya conse ndi madzi onse, zimene zinali mcirikizo; munthu wa mphamvu, ndi munthu wa nkondo, woweruza ndi mneneri, ndi waula, ndi nkhalamba, kapitawo wa makumi asanu ndi munthu wolemekeza, ndi mphungu ndi m’misiri waluso ndiwodziwa matsenga. Ndipo ndizapereka ana akhale akulu awo mwacibwana adzawalamulira. Ndi anthu adzabvutidwa yense ndi wina, yense ndi m’nansi wace mwana adzadzinyaditsa yekha pa akulu ndi onyezeka pa olemekedwa. Pamene mwamuna adamgwira mbale wace m’nyumba ya atate wace, nadzati, lwe uli ndi cobvala khala wolamulira wathu, ndizapasula kumeneku kukhala m’dzanja lako:**

**Tsiku limenero adzakweza mau ace, kuti m’nyumba mwanga mulibe cakudya kapena cobvala; inu simudzandiyesa ine wolamulira anthu. Cifukwa kuti autse mkwiyo wa m’maso a ulemerero wace. Maonekedwe ankhope zao awacitira iwo mboni, ndipo amaonetsa ucimo wao monga Sodomu. Saubisa. Tsoka kwa moyo wao! Cifukwa iwo anadzacitira zoipa iwo okha. Nenani za**

wolungama, kuti kudzamukomera lye; macitidwe ao. Tsoka kwa woipa! Kudzamuipira; cifukwa kuti mphoto ya manja ace idzapatsidwa kwa iye. Anthu anga awabvuta ndi ana, owalamulira ndi akazi. Anthu onga inu, iwo amene akutsogolerani, ndiwo akucimwitsani naononga njira zanu zoyendamo.”

Nthawi idzafika mwamsanga pamene umoyo wopanda Mulungu udzakhala katundu wosanyamulidwa m'magulu a anthu okhalamo, kotero kudzitamandira ndi kudzitukumula kudzamira. Kudzakhala kuti kudzichepetsa, kudzabwerera. Ndipo cifukwa kuzakhala nthawi zonse okhulupirira okhalira omwe ali ndi mtendere mkati mwa miyoyo yao, ofulumizika kuyamba kumverera kwa iwo ndi kupeza machiritso, chitsitsimutso cingathe kuyamba mu anthu m'manambala ochuluka kubwerera kuchikhulupiriro mwa Mulungu wa moyo amene tingathe kudziwa kudzera m'mwana wake Yesu Kristu, yekhayu woona ndi wopambanirathu kugonjetsa, mphunzitsi kuchiritsa zironda za mtima. Yesaya 9:6-7, Uyu ndi uneneri wakubwera kwa Mphulumutsi, Ambuye wathu Yesu Kristu, wokondedwa **“Wodabwitsa Mphunzitsi”**. Mverani! **“Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa kwa ife mwana wa mwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lace, ndipo adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu Wamphamvu. Atate wosatha Kalonga wa mtendere. Za kuonjezera ulamuliro wace, ndi zamtendere sizidzatha pa mpando wacifumu wa Davide ndi pa ufumu wace, ku ukhazikitsa ndi kuuchirikiza ndi ciweruziro ndi cilungamo kuyambira tsopano ndi kunkhabe nthawi zonse. Cangu ca Yehova wamakamu cidzacita zimenezi.”** Utumiki wa Yesu Kristu unayambira mu Galileya ndipo anawerenga mubuku la Yesaya m'sinagoge ku Nazareti. Anawerenga uneneri wina Yesaya ananena za lye kuti

adzaciritsa mitima yotsweka, tipeza izi mu, Yesaya 61:1-2 ndi Luka 4:18-19, akuti, **“Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa Ine; pakuti Yehova wandidzoza Ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndimange osweka mtima, ndikulalikira kwa am’nsinga mamasulidwe ndi kwa omangidwa kutsegulidwa kwa m’ndende, ndikalalikire caka cokomera Yehova ndi tsiku lakubwezera la Mulungu wathu, ndikatonthoze mtima wa onse amene akulira maliro.”**

Sipanakhale mphunzitsi wopambana padziko lapansi kopambana wogonjetsa Mulungu. Ndaphunzitsa tsopano muno mu Afilika, **“Machiritsidwe azironda mtima wobvulazika”** kwa zaka khumi ndi cimodzi m’ndende ndi m’madera ndi m’machalichi ndipo ndapeza kuti ziphunzitso zotsatira zatulutsa mayankho kwa odzichepetsa ndi akhalidwe la umwana ofuna kudza kwa Mulungu yekhayu ndi mphunzitsi ndipo amachiritsa zironda za mtima wotsweka ku mizimu, m’kwiyo, kuilola kupita ndi chizondi cace ndi cinyengo kotero kuti Mulungu abwerera kwa iwo ndi kumanganso umphumphu ndi coonadi m’kati mwa mtima, koposa kuwathandiza anthu aphunzire kuyanjana ndi mabvuto awo.

## 9. MULUNGU ACHIRITSA ZIRONDA MUMTIMA

Machiritso samabwera popondereza zikumbumtima za zophweteka za zoipa zinacitika mu miyoyo yathu koma kumakumana nazo ndi kubvomereza zokwiyitsa kwa anthu amene anatikwiyitsa ndi kutiphweteka ndi kutikana ife ndi kupempha Atate Mulungu conde atikhululukire ife tsopano ndikutichotsera m'kwiyo mkati mwa mitima yathu.

Zironda za mitima, ya mathupi athu yauzimu yali monga zironda mumathupi yathu ya cilengedwe, mathupi awa amaoneka mofanana ndikuti amatha kumazindikirana wina ndi m'nzake pamene akumana kumwamba mu ulemerero wa Mulungu. Ngati tiri ndi kutemedwa ndi kumanga bala lija kufikira litaima kutuluka magazi, ndipo ngati sitichitapo kanthu' ife m'nthawi tidzasowa dzanja lonse. Conco, ncimodzi-modzi ndi thupi lathu la uzimu, mabala omwe sanasamalidwe yatha kumaonongeka kweni-kweni. Maukwati akutha pambuyo pa zaka zabwino ndi citsanzo, za zironda zakale za mtima kuchokera kale kukhala chirimbikitso. Zironda za uzimu ziyenera kusamalidwa, kuikidwa mankhwala, kusoka mabala kuti zitseke kuikapo mafuta ndi bandeji kuti machiritso ayambe.

Kubvomereza kuti ndife ocimwa chikhala cabwino kukhala njira yozikhutula pamaso ya Mulungu, koma sikupereka machiritso a ucimo wapadera. Yakobo analemba mu, Yakobo 5:16. **“Cifukwa cake mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupemphere wina kwa mnzace kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungamo likhoza kwakukulu m'macitidwe ace.”** Pamene tibvomereza zolakwa zathu kwa wina ndi mnzace, ndikubvomerezanso kwa Atate wathu wa kumwamba, ubwenzi wathu ndi Mulungu ndi azibambo uzasintha kotheratu ndipo machiritso azatenga malo muuzimu ndi mthupi.



Ndaphunzira mwapadera mphamvu ya mau omwe tilankhula comwe amapanga. Conde pangani kubvomereza ndi milomo yanu, mokuwa, mulole achokere munsu mwa mtima wanu. Aroma 10:8-10, anena momveka bwino, **“Koma citani, mau ali pafupi ndiwe, m’kamwa mwako, ndi mumtima mwako; ndiwo mau a cikhulupiriro amene ife tiwalalikira, kuti ngati udzabvomereza m’kamwa mwako, ndi mumtima mwako Yesu ndiye Ambuye ndikukhulupirira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa udzapulumuka. Pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilingamo ndi m’kamwa abvomereza kutengapo chipulumutso.”** Ndiringirira ngakhale m’mene Mulungu adalengera zinthu zonse kudzera m’mau olankhulidwa, palibe cidatengedwa koma kudzera mwa Ambuye Yesu Kristu, mau. Mwaici, machiritso abwera mwaubwino ngati ife tibvomereza ndi kupemphera mokhuwa.

Ndichodabwitsa pamene tisintha **“Pakuiwala zomwe zinaticitikirira ife.”** Kudzanso **“Kukhululukira otilakwira zimene anaticitirira ife.”** Mukwiyo ndi kuphweteka udzacoka ngakhale tizikumbuka, tapeza coona ndipo sazatilakwiranso m’njira imodzi-modzi, pamene Mulungu abwerera m’zirona zathu zakale m’chigawo ca uzimu ndi mtendere ndi mopitirira machiritso a mzimu ndi thupi. Yesu sanalankhule mwacabe, **“Mtendere Ndikupatsani, mtendere Wanganga ndipatsa inu.”** Iye ndi mphunzitsi, M’chiritso ndi wopereka mkati mtendere.

Ndicothandiza tikazindikira otilakwira ndipo tiri m’cifundo cacikhululukiro cifukwa tonse tinacimwa ndipo tifuna cifundo ca Mulungu. Ngakhale m’dani waipitsitsa afunika ici, ndipo Yesu anamfera nayenso. Sichotheke kukonda Mulungu Atate ndi kuda ana ake am’njira amene amkondanso Yohane analemba 1 Yohane 2:9. **“Iye amene anena kuti ali m’kuunika, amuda mbale wace, ali mumtima kufikira tsopano lino.”** ndipo mu,

1 Yohane 4:20 **“Munthu akati, kuti, ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wace ali wabodza, pakuti iye wosakonda mbale wace amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona.”** Cinathandiza kumvera kuti tinacita macimo ife temwe cifukwa sitinakhululukire ndipo tayamba kuphweteka anthu cifukwa nthawi ina tinabvulazidwa m’njira imodzi ndipo sitinakhululukire. Ndipo tilakwira akutiphweteka ife cifukwa iye nayenso ndi wolakwiridwa m’masiku akale ndipo sanakhululukire. Ndife anthu amene kawiri-kawiri tikhala olakwiridwa ndi ucimo wathu wacibadwidwe ngati tamva kukanidwa ndi Mulungu achirola ngati tigwiritsa miyeso yosiyana pa ife, koposa iwo otilakwira. Ngati tifuna cifundo ca Mulungu pophweteka wina, ndiye tizafunanso Atate kuchulukitsa cifundo kwa iwo wotiphweteka. Kodi Yesu ali womveka pamene anatiphunzitsa pemphero la Ambuye! **“Mutikhululukire macimo athu monga nafenso tikhululukira adani athu?”** kodi muzindikira kuti m’pempherori mupasa Mulungu cirolezo kuti asakhulukire inu ngati simukhululukira ena? Kodi mulinso mupempherori malire a nthawi pamene inuyo simufunika kukhululukira? Ndizosadabwitsa kuti Yesu aphunzitsa ife kukonda adani athu ndipo acita ici, Iye mwine pokhululukira Afarisi amene anam’khoma Iye pa mtanda ndi kucita naye mayere pamene anali kupacikidwa pamenepo mkuwawa kumene sitingawerengere muyeso wake.

Mika, analemba mwapadera mu, Mika 6:6-8 Amati, **“Ndizafika kwa Yehova ndi ciani, ndiwerema kwa Mulungu wa m’Mwamba? Kodi ndifike kwa Iye ndi nsembe zopsereza ndi ana ang’ombe a caka cimodzi? Kodi Yehova adzakondwera nazo nkhosa zamphongo zikwi, kapena mitsinje ya mafuta zikwi khumi? Kodi ndipereke mwana wanga woyamba cifukwa cakulakwa kwanga, cipatso**

**cathupi langa cifukwa ca kucimwa kwa moyo wanga? Iye anakuuza munthuwe, comwe ciri cokoma, ndipo Mulungu afunanji nawe, koma kuti ucite colungama ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzicepetsa ndi Mulungu wako.”**

Mu Masalimo 51:5-6, mfumu Davide abvomereza ucimo wake woipitsitsa pokhala ndi m’silikali wake **Uliya** kuphedwa kotero angathe kukwatira mkazi wa **Uliya**, Batisheba, Davide alemba **“Onani ndinabadwa m’mphulupulu: ndipo mai wanga anandilandira m’zoipa. Onani, Inu mukondwera ndi zoonadi m’malo am’tseri mudzandidziwitsa nzeru. Mundiyeretse ndi hisope ndipo ndidzayera; munditsuke ndipo ndidzakhala wambu woposa matalala.”** Davide anamvetsa zotuluka zamachiritso m’ndondomeko yakumwamba ya Atate imene azakwaniritsa mwa Iye momwe analembera m’chaputala 13, **“Pomwepo ndidzalangiza ocimwa njira zanu, ndipo olakwa azabwera kwa Inu.”** Davide anapita m’kuciritsidwa kwapadera mumtima mwake pamene analapa ndi kubvomereza mwamphumphu macimo ake ndi kupempha Mulungu akhululukire iye, ndipo demoni wakhale uja amene anayeretsedwa, anaciritsidwa ndi kulumikizidwanso ku mzimu wake ndi Atate wake.

Ine **Kees Hoek**, ndiri ndi zironde zakuya mu mtima zokumba kukhala kale pamene ndisanabadwe. Ndinamva kufulumikizika osamangirizika, ndeka pamene ndinali m’bale wanga mkulu ndi alongo anga awiri ndipo ndinamva kuti panalibe wondisamala ine. Zimenezi nthawi ina zinachoka, maka-maka nditalola Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi, koma zinabwerera ndipo zazunza moyo wanga ndi masiku ambiri. Nthawiyi sindinadziwe cifukwa ninji ndinali nakumvera kumeneku, osamvetsa codzetsa zimenezi. Satana sanafune ine kukumbukira, kudziwa ndi kumvetsa, inali mbali ya Mulungu woumba tsogolo yanga

kuti ndikakwaniritse colinga cake mwaine kubweretsa uthenga wamachiritso a mtima wobvulazika uzimu wanjala mu Afilika.

Davide tsono akusonyeza kubvulazika ndi mzimu wa mkwiyo umene unapatukana kapena upasukana monga mu Malsamo 51:16-17, **“Pakuti simukondwera ndi nsembe, mwenzi nditapereka, Nsembe yopsereza simuikonda. Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka; Inu Mulungu simudzaupeputsa mtima wotsweka ndi wolapa.”**

Paulo alemba mu 1 AThesalonika 5:23-24 **“Ndipo Mulungu wantendere yekha ayeretse inu konse-konse ndipo mzimu wanu ndi moyo, ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu zopanda cirema pa kudza kwace kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. Wakuitana inu Ali wokhulupirika amenenso adzacicita. Amen.”**

Mau a Mulungu anena m'malo ambiri zakutsweka kwa mzimu, kuti mizimu yathu iri mziduswa. Tikasunga mkwiyo ndikutenga modekha, mzimu kwa wina wotiphweteka, Mulungu wathu amatembenukira mbali ija yathu popeza amakonda otirakwira ndipo Yesu anafera munthu ujanso. Cimeneci chipatsa satana mphata wofulumiza mbali yathu ndikupatulula ico kucikumbu mtima ca mzimu, kuticotsera komwe tiri ndikuyamba kukhala umoyo wa ico cokha. Gawolo likhala la demoni ndipo yemwe satana amagwiritsa nchito ndi kuononga ici. Ndiye momwe zinakhallira mu umoyo wanga utali ndi cizunzo cacikulu, maka m'maloto usiku. Ndinamvanso m'masana, kuti ndinafulumizidwa, kwambiri nthawi yocepa. Ici cinaoneka m'kayendetsedwe kaukali ka galimoto m'miseu ndi pocita zinthu popanda kusunga danga loyang'anira zoipa. Ngati mwana wachicepere ndinali m'ngozi nthawi zonse, banga limodzi lisanacire, lina lipezeka. Ndinafunitsitsa kucita bwino koma pafupi-fupi sinakatero. Mulungu wathu ndi Woyera, ndipo

sadzayanjana ndi mizimu yokwiya mkati mwathu koma aitana ife kuti ituluke. Khalani oyera pakuti ndine Woyera.

Mungathe kuona tsopano cifukwa Davide akulankhula pa kathyoredwa, ndipo Paulo alemba kuti mzimu wathu ukhale woyeretsedwa, upangidwa oyera, osati cabe mbali. Mumvetsa tsopano pamene tilankhula pa kugawanika kwa chikhalidwe ndi cifukwa anthu ambiri ophwetekedwa amakhala ndi zikhalidwe zambiri zimene ziri zangozi kutuluka m'zironda m'mitima yathu imene tapatuka kwa iyo? Sitingakumbukirenso zimene zinacitika, kapena kumvera kuphweteka nthawi zambiri, koma chikhalaria zinawacitikira ndi mtima wophwanyika mwaife. Mungaone m'mene tikhalira wasathandizika. N'chabwino kuti palibe muyeso woikika pakukhulukira otilakwira, koma tingakhulukire iwo bwanji ngati sitikumbukanso?

Satana safunanso ife kukumbukira zodzetsa ndi chikhalidwe ca zironda, koma tiyenera kucita izi ndipo satana azataya mphamvu paife. Tipeze coonadi ca izi mu, Yeremiya 17:9-10. **“Mtima ndi wonyenga koposa, ndi wosacitiritsika, ndani angathe kuuzidwa? Ine Yehova ndisanthula mtima ndiyesa imso, kuti ndimpatse munthu yense monga mwanjira zace, monga zipatso za nchito zace.”** Satana amafulumiza pa kugawa zigawo za mzimu wathu, inde kupasuka kudzera kumverera kumene lye atipatsa ife ndi pamene iye afunitsitsa ife kuti tiganize, tikhulupirire ndi kucita. Chitetezo ku mizimu iyi ndico mizimu yathu yogawanikana, ikhala miyoyo ya iyo yokha, lekani ipite ndi chinyengo ndi mkwiyo kotero kuti ikayanjane ndi Mulungu ndi mzimu wathu. Atate wathu atha upanga ife kukhala woyera kuchiritsa mtima wobvulazika, ngati tiri ofuna kudzicepetsa ndi kugwirizana naye. Paulo analemba mu, 1 Athesolonika 5:23-24, **“Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konse-konse, ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu lisungidwe zamphumphu zopanda**

**cirema pakudza kwace kwa Ambuye wathu Yesu.”** Inde lye adzacitha.

Kelementi mu, Ahebri 12:14-15, aitana iye izi zopasuka za mzimu, “Mizu ya kuwawa”. **“Londolani mtendere ndi anthu onse ndi ciyeretso cimene, akapanda ici, palibe m’modzi adzaona Ambuye. Ndikuyang’anira kuti pangakhale wina wakuperewera cisomo ca Mulungu kuti ungapuka mu wina wa kuwawa mtima, ungabvute inu ndipo aunyinji angadetsedwe nao.”**

Miyambo 3:5, iyi ndiyofunika kwambiri pa kumvetsa njira ya ciyero **“khulupirira Yehava ndi mtima wako wonse, osachirizika pa luntha lako”**. Iye azakupambanitsa iwe popanda kulakwa kulikonse. Ngati tichita zomwe ndi Mulungu wathu ndi Atate, ndi kuyenda mu ubwenzi ndi m’chikondi ndi lye, kuzanso ndi ulemu, ife tizakhala pansu pa ulamuliro wake cabe, sanganyengedwe ndipo kulandira coonadi, m’ mzimu wanzeru: Kuopa Yehova ndiko ciyambi ca nzeru; (Masalmo 111:10, Miyambo 9:10), concu, tingakumbuke bwanji zonse zinacitika mbuyo zimene zinakhuzza ife kwambiri? Mulungu adziwa mitima yathu, ndipo ndibwereze Yereimiya 17:10, **“Ine Yehova ndisanthula mtima ndiyesa imso kuti ndimpitse munthu yense monga mwa njira zace, monga zipatso za nchito zace.”** Davide anadziwa pomwe analemba mu Masalmo 124:8, **“Thandizo lathu liri m’dzina la Yehova wolenga kumwamba ndi dziko lapansi.”** Athandiza ife kukumbukira zathu zakale ndipo akudikhira zigawo zokhumudwitsa mwa ife kubwerera kwa lye, kupempha lye chikhulupiriro ndi kukhululukira adani athu. Kotero zigawo zathu zobvulazika zidzakhazikitsidwanso mwa ife, kutsogolera moyo wathu kukacita zinthu zoyenera, ndi chikondi, chifundo chopitirira kwa adani athu ndi kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wathu.

Tingathani ife, ndi thandizo la Atate Mulungu wathu, kupeza mabvuto obisala m'mitima yathu?

1. Pemphani Mulungu abvumbulutse kwa ife bala lobvulazika ndi kupweteka m'mitima yathu.
2. Pezani gwero la kuzunza kaya chiwawa zimatidzera m'maloto ndi njira zina.
3. Pezani zimayambitsa kupondereza maganizo.
4. Pezani zifukwa zodzetsa ifeyo kuwawidwa ndi anthu ena, momwe tidziwika nao kwambiri ndi kuyambana nao powakwiwira iwo.
5. Kumvera mau kuchokera ku mizimu yogawanikana kulankhulana za ife.
6. Anthu ena, abwenzi ndi banja, angathe kuona mabvuto mwa ife omwe ife sitingathe kutero. Mobwereza, sangathe kumva magwero ake, koma azindikira za khalidwe ndi zolakwa koposa momwe tingathero. Ngati afuna kulankhula izo ndi ife, musayese kumverera kwa iwo.
7. Kuwawa kochuluka kunayalidwa m'mitima yathu, mochuluka tidzakala olamulira anthu. Cifukwa pali kufunika kwa cilengedwe kukhala ndi anthu pa mtunda wodekha kuti tikasunge muyeso wa mamvedwe akuwawa pansu. Kupezeka kwa anthu ena pa iwo wokha angadzitse kumamvera mobvuta mthupi.
8. Kuposatu, abambo amakhala aukali m'zonse iwo akucita, kuonjeza pamene akuyendetsa galimoto m'miseu. Iwo sazatsatira; koma iwo mwa mwano azadutsa nukhala patsogolo pa iwe. Lero tiona zimenezi ngakhale mwa akazi. Kwa azibambo, misonkho ya magalimoto imakhala

yodula kuposa mopitilira misonkho ya azimai koma m'zaka zatsopano zimenezi zasintha kweni-kweni.

9. Munthu wobvulazika amapereka zochepe cifukwa ca kuchepekera kwa chikondi. Yesu analankhula pa mutuyu mu Mateyu 6:22-23, **“Diso ndiro nyali yathupi: Cifukwa cace ngati diso liri la kumodzi, thupi lako lonse lidzakhala lowalitsidwa.”** Pakati pa maiko a Aluya (Middle East), mau okuluwika, munthu ali ndi diso labwino ndi mfulu woposa. Ndipo Yesu anati: “Koma ngati diso ndiroipa, thupi lonse lizakhala mu mdima. Ndipo ngati kuwala kuli mwainu ndi m'dima, kupambana kwake kwa mdima kukhala kotani?
  
10. Ngati tiri ndi bvuto kukonda anthu ena, ndi cifukwa cinthu cina sichinatanthauziridwe bwino kwa iwo, ciyambi m'cikumbumtima kutikumbutsa za bvuto lalikulu mwa ife. Ndikumbutsidwa za Yesu mu, Mateyo 7:1-5, akunenena kuti, **“Musaweruze, kuti mungaweruzidwe. Pakuti ndi kuweruza kumene muweruza nako, inunso mudzaweruzidwa ndipo ndi muyeso umene muyesa nao, kudzayesedwa kwa inunso. Ndipo upenya bwanji kacitsotso kali m'diso la m'bale wako, koma mtanda uli m'diso la iwe mwini suuganizira? Tandilola ndicotse kacitsotso m'diso lako; ndipo ona, mtanda ulimo m'diso lakoli wonyenga iwe! Tayamba kucotsa m'diso lako mtandawo, ndipo pomwepo udzapenyetsa kucotsa kacitsotso m'diso la mbale wako.”**

Paliponse ndikomana ndi wina ndipo pali cinthu cina ca iye codzetsa ine kumva kuwawa, ndaphunzira kupempha Atate Mulungu comwe ciri cifukwa, popeza cingakhalenso cobvulaza cina mtima wanga ico Ambuye afunabe kundionetsera ine.



## 10. CHISANU CABWINO CA PASAKA.

Timasangalala caka ndi caka, Cinai coyera ndi cisanu cabwino pakuti masikuwa Yesu anachititsa Pasaka wothera pakudya ndi ophunzira ake cakudya ca m'madzulo ndi imfa yake ya pa mtanda cifukwa ca macimo athu. Yesu ndi ophunzira ake acurukitsa modabwitsa kumasulidwa kwa Israyeli ku nsinga zake ngati akapolo mu Aigpto pa kupereka nsembe yopanda banga ndi poika mwazi wake pa zitseko za manyumba yao ngati cikhalidwe ca kumasulidwa kwao. Koma Yesu anayang'ana momwe, mcifuno ca Atate ake m'kukwaniritsidwa kwa nthawi, lye tsopano ndi nkosa yangwiro ya Mulungu, yopanda banga, amene azamasula anthu kuzipsinjo za ukapolo wa satana pokuyendetsedwa ndi lye. Cizafunika kuti Yesu akapereke moyo wake munsi tsopano cifukwa ca ife tonse. Nthawi ino, lye ali ndi maganizo, ululu waukulu pa zimene Atate wake afuna lye apitemo m'maola makumi awiri ndi anai (24 hours). Koma ophunzira ake kufikira samvetsa cimene mphunzitsi wao ali m'kucita ndipo ali mkumenyana za yemwe akhale pa dzanja lamanja la Yesu pamene akakhale mu ufumu ndi lye. Palibe yemwe afuna kusambitsa mapazi awo atengeko mbali mkutumidwa. Ngakhale nchitoyi Yesu ankatenga, kuwaphunzitsa phunziro limodzi la, **“Wamkulu mu ufumu wa kumwamba ndi mtumiki wa onse.”** Ndipo tsopano amaliza cakudya ca m'mazulo ndipo Yesu akuti: “bwerani, tiyeni titsamuke.” Akupita pamwamba pa Chipinda pomwe ankaona cidikha ca Kidiloni ndi dimba la Getsemani kumapazi a Phiri la Olivi. Mbuye wathu anakomana kuja mobwereza-bwereza ndi ophunzira ake. Kuwawa mwa Yesu kunaumbidwa ndipo Yudasi am'cokera kale kukampereka lye ndi makobidi. Ndithu kulingalira lye kunyamula maso kumwamba ndi modabwa: “Yudase ukundipereka lye monga analosera, pamene ena mwatsopano apa azamwazika, ndipo Simoni Peturo

azandikana kuti sandidziwa Ine. Ndawakonzera iwo tsopano kwa zaka zitatu kukalalikira uthenga wabwino, koma onse ali kuthawa. Atate, nciani comwe cidzakhala mu ufumu wanu?”

Kodi timvetsa mphamvu zatsopano? Yesu akonzeka kutenga ucimo wa ife tonse pa Iye yekha ndi kulipira cilango ca imfa, koma tiri kuthawa kuchoka kwa Iye kuti tisamalire kumasuka kwa miyoyo yathu. Izakhala cisanu kwa ife lamawa, koma izakhala cisanu cabwino kwa Yesu?

Kupenya pamwamba akuona munda wamphesa pamwamba pa mutu wopanga tsindwi la Chipinda capamwamba kupereka mthunzi ku dzuwa, ndipo akuyamba kutsazikana molankhula ndi ophunzira: **“Ndine Mpesa weni-weni ndi Atate wanga Ndiye mwini Mpesa: nthambi mwa Ine imene sibereka amaisadza kotero kuti ikabereke zipatso zoculuka. Inu akuphunzira anga, muli oyera kale cifukwa camau ndalankhula nanu. Khalani mwa Ine ndipo Ine ndikhale mwa inu. M'mene nthambi siitha kubereka zipatso pokhapo ikhala yolumikizika ku Mpesa, kotero simungabereke zipatso pokhapo mukhale mwa Ine. Ndine Mpesa ndipo ndinu nthambi. Iye akhalebe mwa Ine ndipo Ine mwa iye azabereka zipatso zochulukana popanda Ine simungathe kucita kanthu.”** (Yohane 15: 1-5). Masabatha ocepa atapita, Yesu anasimikizira ici pamene ophunzira anali kuweza nsomba usiku wonse kunyanja ya Galileya popanda cogwirapo; Yesu anapereka kugwira nsomba kwakukulu, kuonetsa kuti kopanda Iye sitingathe kanthu.

Nthambi zopanda zipatso zizadulidwa. Analankhula moonjeza “Ndinu oyera kale cifukwa ca mau ndalankhula kwa inu”. Cifukwa akutero Iye; Cikuoneka kuti sakulumikiza ndi kusadza nthambi. Mwaona kulankhula za ku sadza kubereka zipatso. Anali kulankhula zakuchiritsa mitima yathu yobvulazika;

kubvulazikaku kupondereza kusewenza momasuka kwa Mzimu Woyera amene akhala mwa ife. Kumene zobvulazazo zichiritsika, ndiye tibereka zipatso zoculuka mwa Yesu Kristu tikalira.

Pamene zikuyenda muni kukakumana naye m'malo a Getsemani kumene Yudas azakumana naye ndi gulu la akusamala tempile kuti akam'gwire lye, Yesu alankhula ndi amuna ndi kumvera kwakuru koposa kale kotero akhale pafupi ndi lye pamene apita, momveka bwino ndi kwa lye: "Onani, tsopano mukulankhula komveka, tsopano tidziwa kuti mudziwa zonse. Mwaici, tidziwa kuti munacoka kwa Mulungu."

Kamodzi, m'dimba la Getsemani, akusiya ngakhale wokondedwa ophunzira ake atatu akhulupirira kumbuyo ndi kukachonderera nthawi yothera ndi Atate ake. Yesu akuti kwa lwo, "Moyo wanga uli m'cisoni cacikulu conga kuimfa, conde khalani pano ndipo m'khale m'maso nane." Ndipo atapita nthamphulo zingapo patsogolo anagwa pansi mogwada ndi kumadandaulira; Atate ndi Inu, zonse zinthu nzotheka, conde tengani chikhoci kundicokera lne, koma osati kufuna kwanga koma kufuna kwana kuchitidwe." Ndipo mkuwawa kwa kukuru kwa lye, thukuta la magazi linacoka koma anamverera Atate ake kufikira nthawiyi, pakusankha kupereka moyo wake cifukwa ca ife, nkhusa zace. Ndipo apafupi ophunzira ake ngati nkhusa. Uyu ndi Yesu, Cisanu cabwino? Ndicolingalira kuti Yesu anasankhula kuzipereka nsembe pakumverera Atate ake pamene ali mkuwawa kwakukuru. Pothera, ikhala Cisanu cabwino kwa Yesu, Atate Mulungu ndi kwa ife, nafenso pambuyo pakulira. "**Kwatha**" ndi kukhulupirira Atate ake, ndikupereka mzimu wake kwa lye. Anamverera Atate ake kufikira nthawi iyi ndi kumaliza nchito yake yakutilumikiza kwa lye ndi Atate Mulungu wathu. Kodi alipo wokakhulupirira Atate motere?

M'mawa tsiku la Pasaka, Yesu anauka kwa akufa ndipo cifukwa ca ici tidzaukitsidwa kwa akufa ndi Iye. Inde, tikonda kuchukitsa pasaka m'mawa mwake, koma tiri ofuna kupatsa Yesu Cisanu cathu cabwino? Ngati atiitana? Ndife ofunabe kukhalabe mwa Iye pakudzikaniza? Ndi kutenga mtanda wake pa Cisanu cathu cabwino modzichepetsa kwa Atate wake? Tero, anasenza zipatso zochuluka ku ulemerero wa Atate wathu. Kodi tifuna Yesu Kristu aumbidwe mwa ife m'mene Paulo analemba Galatiya 4:19, **“Tiana tanga, amene ndiri kumvanso zowawa za kubala inu, kufikira Kristu aumbika mwa inu.”**

Cisanu cabwino cinali chikumbutso ca tsiku mu umoyo wa Yesu ndipo m'mene apitirira kuumbidwa mwa ife ndipo tipitirira kukhalabe osangalala mumoyo wathu. Pemphani Mulungu aike chikondi cocuruka m'mitima yanu kotero kuti muzafuna kupereka moyo wanu kwa Iye. Kuno ndikusanduliza kwa mau a Yesu mu Mateyo 5:3 **“Odala ali osauka mumzimu; cifukwa uli wao ufumu wakumwamba.”**

## 11. PEMPHERO LOCHIZA

Ndisanakutsogolereni kupemphero limene Atate athu nthawi zonse amayankha, lomwe limachokera m`mtima ofunitsitsa, ndifuna ndikupatseni zitsanzo za m`mene Mulungu adayankhira mapemphero a anthu ochuluka.

- Mnyamata wabwino wa chichepere amene adakhala m`ndende kwa zaka zisanu mnthawi yachiwiri ndipo makolo ake mwachidziwikire adalephera kumapita kundende kukamuona. M`zikhulupiriro za Mipingo yathayi zomwe zimakamba za kubadizanso munthu yemwe adachimwa kwa kukulu, koma sanabwerenso kudzam`mbadiza iye. Pamene ndinatsogolera gulu la akaidi m`pemphero la kupempha Atate Mulungu kuti aulule ndi kuchiza zilonda zopweteka za m`mitima yawo. M`nyamata adakumbukira kuwawidwa komwe adalinako pa makolo ake, chifukwa sankabwerenso kundende kudzamuona iye, kwa zaka zisanu. Adapempha Mulungu tsopano kuti amukhululukire chifukwa choyamba kudana ndi makolo ake amene Mulungu amakonda ndi kumuchotsera mkwiyo mtima mwake pa iwo. Taonani! Makolo ake m`tsiku lotsatira nthawi ya 9:00 koloko m`mawa adafika kudzamuona iye.
- M`chaka cha 2013, Ndidatumikira masiku atatu m`ndende ya Samfiya m`dziko la Zambia, ndidatseka maphunziro ndi pemphero lathu lochiza, azibambo makumi atatu ndi azimayi asanu adabatizidwa m`chitsime chosaya kunja kwa m`panda wa m`ndende. Zidachitika motero kuti azibambo awiri omwe adalandira ubatizo adamizidwa kawiri kawiri m`madzi ndi dzanja la munthu emwe sadamuone. Adayamba kupuluputa ndi manja komanso ndi miyendo pamene adalikumizidwa m`madzi ena adathamanga ssm`madzi ndikukatulutsa azibambowa ndi kuwagoneka pa mtunda pamene adali kulimbana ndi ululu kwa ka nthawidi pamene mtendere udawapeza iwo. Patatha masiku awiri azibambo adabwera pamodzi kwa mlangizi

(mkulu) wa m`ndende kumuuzza iye, sitinadziwa kuti moyo utha kukhala osangalatsa ndi mtendere wotere.

- Mlaliki odzozedwa kwambiri amene ndidadziwana naye kale m`ndende yaikulu pakati pa Zambia yochedwa **Rimandi** m`chaka ca 2011 ndi 2012. Pamene adatsogolera gulu la akaidi pa bwalo la ndende mkupembedza Mulungu kodabwitsa. Mchaka cha 2014 ndidakumana naye mkatikati mwa ndende ya chitetezo, ndagwidwa pa mlandu moopseza ndi mfuti ndipo anamuweruza kuti akhale m`ndende kwa zaka khumu ndi mphambu zisanu pogwira ntchito ya kalavula gaga. Adanyengedwa kuti sadapalamule mlandu ndikuti adawuzidwa molakwika. Komabe adamulemekeza Mulungu Atate wake pa kumtumikira m`ndende kwa zaka zinayi: Posachedwa adapatsidwa nchito yokhala tate oyang`anira akaidi.
- Adabwera kudziphunzitsa zanga zomwe zidatenga masiku atatu ku msonkhano wautali, ndipo patsiku lotsiriza pamene ndidayamba kugawana nawo za mabvuto akusintha pa chikhalidwe chosokoneza, adapempha ngati ndikotheka kuti poyamba aperekere umboni wa zimene Mulungu adamuchitira usiku watha. Chadzulo lake latsikuli ndidachititsa pemphero la kuchiza mtima wobvulazidwa, ndipo adaperekera umboni pa zomwe Mulungu adamuchitira.

Adali mlaliki wodziwika bwino padziko lonse lapansi, kwa zaka ndithu, adali Bishop, Bungwe la Mpingo pamene m`chaka cha 1983 adaitanidwa kumudzi kwawo, chifukwa bambo wake adamwalira, adali mfumu yaikulu yampando, woyang`anira mtundu waukulu ndi mafumu ena pansu pa ulamuliro wake. Monga mwana wa mwamuna wamkulu, adabvomera kulonedwa ufumu watsopano, motsatira mwambo wa chikhalidwe, kuyambira patsiku la mwambo wa kudzozedwa, usiku onse wa moyo wao adali kuzunzidwa ndi bambo awo usiku. Chadzulo lake pa tsiku la mapemphero adapempha

Mulungu kuti amukhulukire chifukwa chakukhala paudani ndi bambo wake kwa zaka zonsezo. Usiku wa tsiku lotsatira adali munthu womasulidwa kwa mzimu yoipa. Wosakhalanso ndi mzimu wozunzawo. M'nthawi zambiri za kuperekeramba umboni wake adali kulira kosalekeza chifukwa cha kumasulidwa, mtendere watsopano, ndi mathokozo ake. Ndidakumana naye m'zinda wa Lusaka m'dziko la Zambia m'chaka cha 2018, ndipamene ndidazindikira kuti mzimu woipa sunabwererensho.

- M'chaka cha 2015, m'bambo wachikulire wa ulemu wake adanditsatira nditamaliza kuphunzitsa pa ndende ya Kamwala, mzinda wa Lusaka m'dziko la Zambia, kuti ndimpempherere. Adali atakhala m'ndende kwa zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu (25) padalibe munthu amene adabwerako kadzamuona zaka zonsezi ali m'ndende. Ndidali nditam'dziwa kale monga tate wa ana achichepere am'ndende, ndinamuza, utha kukhala kuti uli ndi mkwiyo ndimakolo ako ndi azimako, sichoncho?. Ndipo adayankha kuti eya ndi choncho. Ndidamuza kuti alankhulane ndi Mulungu pa zomwe adali kudutsamo, ndidamuza kuti anditsatire pa pemphero la kuchiza mtima wovulazidwa. Monga ndimachitira kulikonse ndapita, ndidamuza akalankhule mozipereka. Ndidamuona akulankhula kwa nthawi yaitali, nditamuuza kotseka pemphero lotsiriza. Patapita masiku owerengeka, ndidapitanso ku ndende ya kamwala, anandiuza kuti patapita tsiku limodzi kuchokera tsiku lomwe adapemphera pemphero la kuchiza mtima ovulazidwa, mzake, Kwambiri kuchokera ku mzinda wa Livingstone, mtunda wautali okwana ma kilomita mazana makumi anayi ndi mphambu zisanu (450) adabwera kudzamuona nthawi ya 16:00 madzulo.

Mulungu wathu ndi wamoyo kwambiri, Iye sagona kapena kutitalikira, kapena kutisiya tokha kuchokera atatilenga ife. Makamaka angachitirenji zotisiya tokha, ngati Iye adatilenga m'chimwemwe ndi m'chisangalalo cha Iye mwini. Koma Iye

akudikhira ife kwa thunthu kuti tifike kwa Iye monga mwana wa chichepere, kuti timulole ndi kumukhulupirira ndi mtima wathu wonse. Kodi tsopano Munthu kumupempha kuti akuthandizeni kuti musendere chifupi ndi Iye ndikumulola Iye kuchiza mtima wanu vulazidwa, ngakhale kuti zitha kutenga nthawi yaitali?

Nenani pemphero lomwe ndimatsogolera anthu, kuli konse ndi kulankhula pa chigonjetsochi ndipo Mulungu Atate wanu adzachita chozizwitsa mtima mwanu. M`mawu amene ndilankhula mulibemo matsenga ali wonse, iri ndi pemphero la Munthu payekha la pakati pa iye ndi Mulungu wake. Mupemphere monditsatira koma pokha-pokha zolankhula zanu zichokere pansu pa mtima wanu. Tsono welengani pemphero lonse ndi kuona ngati liri lofunika kwa inu. Mulingalire mozama kwambiri, likhazikike mtima mwanu. Ndipo pamene mupemphera, pempherani mokweza kwambiri zomwe zidzasonyeza kuti zikuchokera pansu pa mtima wanu. Mulungu Atate wathu akudalitseni. Mulungu akupatseni chikumbumtima cha zinthu zowawa kwambiri, musazipondereze kapena kuzibisa, koma muuzeni Mulungu mwachindunji cha zomwe zidachika, ngakhale kuti ndi zinthu zobvuta kwambiri, ndi mbali imeneyo yomwe ili yovulazidwa yomwe ifunika chiyanjano ndi Mulungu, Atate. **“Mulungu ndikuthokazani kwambiri chifukwa chakundikonda mudapereka mwana wanu yekha, kudzafa chifukwa cha machimo anga kuti ndidze kwa Inu. Ndifuna kuti ndikukondeni monga Inu mundikonda ine, koma ndizobvuta kwambiri chifukwa cha zowawa zobisika zamkati mwa mtima wanga, Conde Mulungu ndithandizeni kuchotsa zilonda mtima mwanga zomwe zinditsekereza kufika chifupi ndi Inu? Nthawi zambiri, ndimalakwabe ndipo mkwiyo wanga umakhala pa anthu, sindimakhululuka komanso kuiwala zinthu zonse zachitika.**



**Tsopano, mungandichotsere ine ululu opweteka wa mtima kuchokera nthawi imene ndidalakwa kwambiri?”**

Tsopano mukhale chete ndipo mumvetsere Mulungu mu mtima mwanu. Ndipo pamene mukumbukira kuwawidwa kwakukulu musapondereze izi ngati ndi zopweteka kwambiri, muzithetse izi, tsopano pomaliza ndi Mulungu wanu. Uzani Atate Mulungu zonse zidachitika mutawawidwa, Mulungu akumasuleni ngakhale zikhala zopweteka bwanji. Ndipo mupemphere “kodi sim’amamvetsa chifukwa chomwe ndidamvera kuwawa?” Amamvetsa ndipo amalira nafe limodzi kawiri kawiri. Tengani nthawi yaitali monga mungathere kulankhula ndi Iye. Ndipo ndipemphera pemphero lotseka ndi inu mutatha kudikira kwa mphindi zisanu kapena kuti mapemphero amumtima kuti athe. **“Atate, ndikukuthokozani pa kundichiza, ndiponso pa chikumbutso cha chopwetekachi, tsopano ndiri wachisoni kwambiri, kuti ndidana ndi mkwiyo ndi..... (Lembani dzina la munthu yemwe mwakhala mukumukaikira muno) kwa nthawi yaitali ndikadatha kumuda bwanji.....? Pamene mumukonda iye kwambiri monga m’mene mundikondera ine? Pepani kwambiri. Tsopano ndimvetsa kuti ndi ndani munthu amene, iye adandilakwira chifukwa iye adalackwiridwa chimodzi-modzi pa kukanidwa, kuzunzidwa, ndikuyenera kumuchitira chifundo, poti nanenso ndifuna chifundo chanu, mundikhululukire Mulungu, ndipo Yesu mubwere ndi kukhala mu mtima mwanga? Sindifunanso mkwiyo mtima mwanga. Ndithandizeni kuti ndimukonde, monga inu mumukondera, chonde mumudalitse..... manganso Iye afunanso chifundo chanu? Atate ndikufuna ndipite ndi mafumu onse amene ndiganiza kuti ndidana nawo, ndipo inu mukhale oweruza yekha wa chilungamo, zikomo Atate chifukwa cha**

**chikondi chanu pakundikomera ine ndi kundimasula ine kumkwiyo uwu. M'dzina la Yesu Kristu. Amen**

Pakuti kuchiritsidwa kwa chilonda cha mtima sikungabwere nthawi imodzi, bwerezani pemphero kawiri-kawiri kapena kwa kanthawi mpaka mutachiritsidwa kotheratu. Monga tonse timadzimangira ringa kudzera m'kusakhululukira. Njerwa imodzi pa nthawi imodzi, kutalikirana ndi Munthu, linga limeneronso limatisiyanitsa ife ndi Mulungu. Tsopano tiyenera kupeza machiritso kuyeretsedwa nthapulo imodzi pakanthawi, njerwa imodzi pakanthawi, nthawi yiri yonse umamatire kumasulidwa, m'dzamva kupepukidwa ngati chatha cholemetsa chatulidwa m'mapewa mwanu. Ndipo izo ndi zoono ndipo ndi chifukwa chake Yesu adati; Goli langa ndilofewa, ndipo katundu wanga ndi woepuka. Ngati mulimbikirebe, wosagonja idzafika nthawi pamene mudzalola kuti achize mabala ochuluka azirona zopweteka, mwadzidzi lingalo lizaya kugwa. Zomwe sizidzasonyeza kuti ndiri woyera kotheratu. Zomwe sizitanthauza kuti kumbari ya ife ndi zamuyaya, koma pamene zatero izapanga ife kufika chifupi ndi Mulungu, kudzatipanga ife kukhala ana a Mulungu wokhwima mu uzimu. Paulo adalemba izo m'buku la Aroma 8:14 pakuti onse amene atsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu. Phunzirani kuti lye akutsogolereni, Adziwa bwino lomwe kwambiri za bwino zoyenera ife musachitenso kanthu kali konse panokha, yenda-yendani patsogolo pake, koma lolani kuti Atate akumwamba akutsogolereni nthawi zonse, ndipo akuchitireni chiri-chonse. AMEN

**NDIKHULUPIRIRA  
AKUDALITSENI.**

**MWACHIRITSIDWA**

**AMBUYE**

